

ZIPHUNZITSO

ZA

BAIBULO

UTUMIKI

UTSOGOLERI

NDI

KUKHAZIKITSA (KUDZALA) MPINGO

Okopela Junta de Missões Nacionis

Convenção Batista Brasileira

Rua Ganzanga Gastos 300

Kukopela bukuli ndi koletsedwa chifukwa sikofunika kuonjezera kapena kuchotsera zomwe zili m\bukuli.

Mabuku amene akhala akuluka chipwitikizi ali motere:

1991	mabuku	1,200
1992	mabuku	2,800
1993	mabuku	2,000
1994	mabuku	10,000
1995	mabuku	10,000
1997	mabuku	10,000
1999	mabuku	10,000
2006	mabuku	15,000

Onse pamodzi mabuku ndi 61,000

Mabuku omwe akhala akutulutsidwa muchingerezi ali motere:

1995	mabuku	1,000
1999	mabuku	5,000
2000	mabuku	4,000

Bukuli linasindikizidwa muchipwitikizi pa mutu oti

Utumiki Oyamba

Mlangizi wa zakayalidwe ka mawu ndi zinthuzi: Rogerio Freitas de Oliveira

Otanthauzira kokyamba : Chrissy Akins Brawner

Otanthauzira komaliza : Juan Alberto Galvis

Wotayipa pa komputa : Reynaldo Amaral

Lidakakozedwabe ndi kusindikizidwa m'ziko la Brazil

ZMKATIMU

Chiyambi	4
kuthokoza.....	7
Matanthauzo.....	10
Tingagwiritse bwanji bukuli.....	11
Mfundo: ya buku la atumiki oyamba , Utumiki ndi kubzala matchalitchi	13
Zofunika kutsata: Tingaphunzitse bwanji gulu lanthu.....	45
Mapulani: Njira zokulitsira mpingowu.....	73
Njira zotamandira.....	75
Atumiki oyamba ndi m'mene angathandizire kudziwa baibulo	
Popanda zipangizo za baibulo.....	82

E-mail address: wadeakins@pobox.com

Webuasayiti: <http://www.pioneerevangelism.org>

CHIYAMBI

Nthawi idzafika pamene amuna sadzava zonena za ena. M'malo mwake pofuna kudzisangalatsa adzasonkhanitsa atumiki ambiri kuti adzinena zomwe zikuyabwa m'makutu awo. Adzatseka makutu awo kudana ndi chilungamo ndi kutsata zikhulupiliro za makolo awo.

Koma inu khalani m'maso ndipo imani njii. Gwirani ntchito ya mtumiki ndipo khalani olimba pa utumiki wanu 2 Timoteo 4: 3- 5

Dziko lero ladzadzidwa ndi zonyasa ngati m'mene zinali zaka zilumika zapitazo. Kulemba bukuli ndi chosonyezo chonena zoonna zenizeni za undindo wa aliyense mwa Yesu Khristu mwini wake. Mwa iye chilichonse chotheka.

Ntchitoyi ikhoza kukhala youvuta ngati nkhani yake ikakhala ya atumiki oyamba okha palibe chothandiza za china chili chonse pa nkhani ya atumiki oyamba okha. Cholinga cha buku la atumiki oyamba nkufuna kubweretsa munthu aliyense chifupi ndi Mulungu ngati chinthu choyamba pamoyo wathu.

Dokotala wina wotchedwa Akins anakwanilitsa zotsatira zabwino pokulitsa mpingowu. Iye anakwanilitsa ntchitoyi pogwiritsa njira zakezake chifukwa anali zazo mphamvu zakuthekela.

Malamulo a baibulo abwera kwa ife ndi cholinga chomwecho ndipo izi zimaveka ndi mneneri Tomoti yemwe anauzidwa kuti gwirani ntchito yotumikira Ambuye.

Izi zosavuta ndipo ndi chapafupi monga malembo anenera.

Pr. Ivo Augusto Seitz, Mlembi wankulu wa mpingo wonse wadziko la Brazil.

ZOTI TIZIDZIWE

Sherry Deakins Akins ndi amene ali munthu oyamba amene anamulimbitsa Thomas Wade Akins kudzera mwa mphamvu ya Mulungu amene anayambitsa ndi kukuza mpingo wa atutmiki oyamba ku Brazil.

Pozindikira kuti kulemba, kusonkhanitsa pa ndondomeko imeneyi imafunika nthawi yokwanira komansosayenera kukhala pafupi ndi banja, Thomas Wade anavutika mumtima ngati kunali koyenera kupitilira ndi nkhani imeneyi. Ali nkati mogawana nzeru ndi mkazii wake usiku wina, bamboo wina otchedwa Sherry adati Thomas Wade uli ndi tchito yaikuluyokuza mpingowundi odzadzidwa ndi mzimu oyera

Mpingowu udayamba kukula pang'onopang'ono ndipo udayamba kufalikira osati mudzinda wa Minas Gerais ku Brazil komwe amakhala kuyambira m'chaka cha 1992

Sherry anadwala matenda otchedwa Schleroderma omwe anagwira mitsempha ya m'mapapu, matumbo ndi mbali zina za thupi.

Atafunsidwa kuti abwere ku United States kukhala ndi banja lakwawo ndi kusiyana nalo dziko la Brazil, iye anayankha kuti “cholinga cha moyo wanga ndikulemekeza ambuye Yesu Khristu munthawi ya moyo wanga wonse kufikira kufa kwanga” Ku Brazil kuno ndiko Mulungu anatiyitana ndipo ndikuyenera kukhala konkuno.

Mwadzidzi Sherry angwa pansu ndipo anamwalira ku nyumba kwawo ku Belo Horizonte, Minas, Gerais, Ku Brazil. Sherry anali m'modzi mwa emene anakhala ndi kumwalira m'chifuniro cha Mulungu.

KUDZIPEREKA

Ndikudzipereka kwathunthu mu Bukuli kwa mkazi wanga okonedwa Barbara Ann Hawthorne, amene ali mphatso yochokera kwa Mulungu ya ine.

Zonse zabukuli sizopeka ayi kwa Barbara koma wakhala akugwiritsa ndipo akugwiritsidwa ntchito ndi mzimu ogonjetsa komanso wobzala mpingo. Mulungu watidalitsa ndi kutilora ife kutumikira tonse komanso kuphunzitsa ena mwa atumiki oyamba mu nkumano mu Brazil yonse komanso dziko lonse lapansi

Thomas Wade Akins

KUTHOKOZA

Bukuli silikanatheka popanda kudzipereka kwa moyo kwa kachenjede wotchedwa Cal Guy. Iye ndi njira zake za ukadaulo adatiphunzitsa njira za makono.

Izi zidatithandiza kuti pomatha zaka zitatu ndikhale ndikudziwa chomwe ndikuchita, kusukulu yophunzilirako za uzimu imene idali kumwera chakuzambwe ndidasiya maphunziro apamwamba kwambiri mu zinda wa ukulu wa Brazil ndikupita ku minda kukatumikira.

Mumakalata ake osalekeza komanso mapemphero akhale ali dalitso waukulu kwa ine.

Izi zakhala zikugwiritsidwa ndi Mulungu kundilimbikitsa pa nthawi yomwe ndinakumana ndi zovuta. Mu nzeru ndi ziphunzitso zake zafalikira paliponse bukuli.

Ndikuwanyadiranso akadaulo omwe adandiphunzitsa pa sukulu ya ukachenjede ina yachedwa Louisiana, ku sukulu zatsopano za zauzimu zotchedwa Orleans ndi yomwe idali kumwera cha kuzambwe.

Kudzera maphunziro omwe ndidaphunzira sukuluzi ndidaphunzira kufufuza komanso kulemba mapilojekiti osiyanasiyana.

Ndiri osangalala kwambiri ndi Dennis Blackmon amene ndi dotolo amene wakhala akundithandiza kukudza maganizo osiyanasiyana bukuli komanso kuthandiza kupereka mfundo zina ndi zina zokuzira mpingowu.

Blackmon ndi amene wakhala akundiitana kwambiri ndi kundilimbikitsa pa nkhani yolembe ndi kugwiritsa ntchito kuyambira poyamba. Maganizo ndi malingaliro ake ndi zofunika komanso zothandiza kwambiri. Kuonjezera pa mfundo zomwe adandithandiza, ndidagwiritsanso zina zochokera mabuku ena monga Mpingo wanakolo yomwe idalembedwa ndi Melvis Hodges, kudzala mpingo wa makoloyolembeedwa ndi Charles Brock ndi ena ambiri.

Dokotala ochedwa Charles Brockndi modzi wa azungu a mishon ku Filipinzi.

Buku lochedwa kudzala mpingo wa makolo lidasindikidzidwa ndi Broadman Press yomwe lidapeleka chilimbikitso chachikulu pa moyo wanga ndipo nazeru za menemu zidali nssanamira za polojekiti.

Dotolo wina wochedwa Waylon Moere adalembe buku nkhani yabwino yochokera kwa ambuye. Maphunziro a mbaibulo amagwiritsidwa ntchito kuchokera uthenga wa Yohane mtumiki wayamba. Moore wakhala akugwiritsa n tchito atumiki

atumiki a mulungu komanso wakhala chifanizo mu moyo wake wonse/mu utumiki wa Mulungu wathu Yesu khristu.

Ndikufuna ndikudziwiseni mchimwene wanga mu dzina la Yesu mkristu, Mario Ikeda, amene adali woyendetsa gawo la utumiki wa gulu lonse Brazil, amenenso adandithyandiza kulemba zones za mbukuli komanso kusonkhanisa zones za pologalanu. Mene ndomasonkhanitsa za pologalamuyi mu nzinda wa Minas Gerais, Mario amasinkhanitsa pologalamuyi mu nzinda wa Para. Popanda Mario wa mu utumiki oyamba mpingowu sukadafika ku dziko la Brazil.

Ndafunanso kuthokoza mtumiki Maizio Penido Bertho mlembi wamkulu wa ku Minas Gerais wa mpingowu. Mtumiki Alizio wakhala akuphunzitsa ndi ine kumaphunziro a zaumoyo kudzera mu dziko lonse la Brazil. Wakhala akundipatsa chilimbikitso chokwanira chokhunza mpingowu mu Manas Gerais makamaka ku mayambiriro pomwe ena mwa maganizo omwe akuluakulu kwa atumiki ndi zikhulupiriro za makolo zomwe sizikhudzana ndi mau a Mulungu.

Mwa chitsanzo buku loyera likuta munthu sangayambitse mpingo ngati sanadzodzedwe komanso ngati katundu kapena nyumba siziri zokonzedwa.

Mau othokoza apite kwa atumiki ose okwana makumi anayi (40) amene agwira ntchito limodzi ku Minas Gerais makamaka pamene tinali polojekiti yoyeselera.

Zaka ziwiri zadali zovuta kwambiri kwa aliyense koma mamishoni 63 ndi amene adali oyambilira ngati zitsanzo za polojekiti. Atumiki amenewa anasunga bwino zimene amafufuza komanso zomwe adapeza pa polojekiti kuti ndindomeko wonse ukhale zadongosolo ndipo zodalilika.

Ntchito omeneyi idathandiza kuti zina zisinthike kuchikera pamene zinaliri poyamba.

Kuwonjezera apo ndafunanso kuthokoza Bill Richardson amene adali mtsogoreri wa mdera lina la ku Brazil pa nthawi imene polojekiti yoyamba imakhazikitsidwa ku Brazil.

Adavomereza za polojekitiyi ndipo zidandichititsa ine kutsogolera gulu loyamba kwa zaka zambiri zoyamba. Mawu okha sangasonyeze kuthokoza kwanga ku Curtis Sergeant, zungu wa Mishoni ku Singapore.

Ine ndi Curtis tidayamba kukondana pamene timaphunzira maphunziro anjira zoluzanitsa ku Sao Paulo ku Brazil.

Mpingo wa Curtis ku tsidya la myanja, maganizo ndi zones zimene amathandiza ndi zamphindu.

Ndafunanso kuthokoza J.O Terry ndi Jackson Day amene adathandiza kupereka magawo ena minkhaniyi. Pomaliza ndafuna kuthokoza abale ndi alongo amene akhala akundithandiza mu njira zosiyanasiyana kutukulu mpingo popanda mantha ndi mosaopa pa umoyo wawo wa uzimu. Anthuwo ndi monga; Dokotala wotchedwa Ray P. Rust amene anali m’busa pamene ine ndinali mwana komanso anali mtsogoleri oyamba kwa ine, m’busa wadziko lonse lapansi wotchedwa Sammy Tippit wochokera ku San Antonio m’busa komanso Dokotala Phill Jett omwe adali mtsogoleri wa Baptist ya Englewood mu nzinda wa Jackson ndipo Tenesi , Mayi nndi Bambo Ronnie Mackey amene anali m’misili wa kasupe wa umoyo , kum’wera kwa Karolina,

Bambo Guy Wolcott, munthu wazamalonda wa ku Portland Oregon ndi David Wilson, President Komanso wotsogolera wa anthu onse apa dziko lapansi

Chikondi change chathunthu chipite kwa ana anga awiri Tim ndi Jason.

Ndafunanso kuthokoza kwambiri nkamwini wanga Jeff Brawner amene anathandiza kwambiri pa Bukuli komanso kuthandiza pa zina ndi zina zofunika m’buku lino.

Pomaliza ndafunanso kuthokoza mwana wanga Khilise amene anatanthauzira bukuli kuchokera ku chipwitikizi kupititsa mu chingerezi komanso analemba chipangano chatsopano ndi chiyambi cha moyo watsopano mwa Yesu. Ndimakukonda iwe Khilise, Tim ndi Hason

Thomas Wade Akins

MATANTHAUZO

CHIYAMBI: Awa ndi mawu amene akutanthauza munthu kapena anthu amene angayambitse ndi kubzala ntchito zachikhilisu komanso machalichi.

ENVANGELISM (UTUMIKI): Awa ndi mawu amene akutanthauza utumiki odzipereka mu uthenga wabwino wa Yesu Khristu.

Mawu akuti pakuti ndimapereka kwa inu poyamba chimenenso ndinalandira kuti Khilisu anafera zoipa zathu monga mwa malembo.

Uwu ndi uthenga wabwino wa malembo oyera umene akuthandiza anthu otaika pa dziko lapansi.

TINGAGWIRITSE BWANJI BUKULI

BUKULI LILI NDI MAGAWO ATATU

- 1. ZOYENERA KUZITSATA**
- 2. ZOYENERA KUZICHITA**
- 3. ZOLINGA ZATSOPANO**

Ziphunzitso: Izi zimatithandiza kufalitsa uthenga wochokera m’buku loyera kuzera mwa atumiki ake za m’mene tingakhazikitsire matchalitchi.

Baibulo ndi buku la mawu ochokera kwa Mulungu ndipo mulungu amatiphunzitsa zoonza zake pa m’mene tingaphunzitsire mawu ake.

Zoyenera kuchita

Njira iyi imatisonyeza za m’mene tingaphunzitsire m’magawo awiri.

Kufalitsa uthenga: Kodi tingayambe bwanji kuphunzitsa Baibulo m’magulu ang’ono ang’ono kapena m’ malo omwe tikufuna kuyambitsa mpingo?.

- Pezani anthu amene akufunitsitsa mtendere wa Mulungu
- Pezani ndi kuchenza nawio anthu amene ali m’chikondi cha Mulungu ameneso mzimu oyera akungwira ntchito yowayandikitsa ndi Khilistu.
- Gawanani nawo uthenga wabwino mundondomeko yakaphunzitsidwe ka baibulo.
- Khazikitsani atumiki atsopano kuzera mu maphunziro a baibulo.

Otumikira: Tingaphunzitse bwanji gulu lanthu kuti likhale lamakhalidwe abwino pa utumiki wawo.

Dongosolo: Iyi ndi njira imene ingathandize kuona m’mene tingachulukitsire anthu mu mpingi. Ndipo tikuyenera kutsatira m’mene Paulo amachitira Timoti 2:2 Phunzitsani ena kuti aphunzitse anzawo.

ZIPHUZITSO ZA M'BAIBULO

(BUKULOYERA)

UTUMIKI (KUFALITSA UTHENGA WABWINO)

UTSOGOLERI

KUKHAZIKITSA (KUDZALA) MPINGO

ZIPHUNZITSO ZA M’BAIBULO, UTUMIKI, UTSOGOLERI NDI KUDZALA MIPINGO

1. KODI KUKHALA OYAMBITSA MU UTUMIKI WOFALITSA UTHENGA WABWINO NDI CHIYANI?

Utumikiwu unayamba m’chaka cha 1989 m’dziko la Brazil, ataphunzira kabzalidwe ka mipingo. Iyi inali nthawi ya Thomas Wade Akin’s mgawo loyamba la utumiki wake ndi a International Mission Board of the Southern Baptist Convention, ndipo anakaphunziranso za chiyakhulo kwa chaka, kenaka anakhazikitsa ndondomeko ya kadzalidwe ka mipingo. Munthawiyi , iye anayambitsa mipingo yokwana khumi ndi iwiri (12) ya Baptist, mu mdzinda wa Minas Gerais, mdziko la Brazil.

Atachoka ku Furlough, Thomas Wade anazindikira kuti utumiki sumapita patsogolo. Iye anaphunzitsa ndi kuwerenga njira zina za kufalitsa uthenga wabwino. Buku la Dr. Charles Brooks lotchedwa **Indigenous Church Planting**, limamuthandiza kupeza zambiri mukafukufuku wake. Kupyolera m’baibulo, buku la Dr. Brooks zina za mbukuli ndinso ndondomeko ya kadzalidwe ka mipingo, Thomas Wade anakhazikitsa sukulu ya utumiki, mgawo loyamba la utumiki wake ku Brazil.

Ndondomeko itatha, abambo ndi amayi okwana makumi anayi (40) anaphunzitsidwa momwe angadalire mipingo. Patapita zaka zopitilira ziwiri, anatekula nthambi zochulukana mizinda yokwana makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zitatatu

Ku MinasGerais. Pamwezi uliwonse kwa zaka ziwiri otumikira amatumiza zotsatita ku Evangelism and Mission Department of Minas Gerais Baptist Convention. Patapita zaka ziwiri gulu linapangidwa lounika utumikiwu. Patapita zaka zitatatu magulu enanso ambiri anakhazikitsidwa, mdziko la Brazil. Abusa, atumiki ndi atsogoleri ena anasankhidwanso utumikiwu.

Zaka khumi ndi ziwiri (12), anakhazikisa matchalitchi mazana awiri (200), nthambi za mpingowu zokwana zana ndi makumi asanu ndi awiri kudza mphambu zisanu ndi zinayi (179) ndi malo ena komwe kumanngolalikidwa okwana mazana atatu ndi makumi asanu ndi atatu nadi mphambu zitanu (383) ku Minas Gerais ku Brazil. Muzaka zonsezi atenga mbali ndi a utumikiwu (Pioneer Evangelism) maripoti. Pofika mchaka cha 200 anthu opitilira zikwi makumi awiri (20,000) aku Brazil, anali ataphuzitsidwa pafupifupi ntchito chikwi (1000) zafalikira kumeneko. Ndipo lero ,magulu a utumikirawa apangidwa m'azana ochuluka chaka chilichonse, kuti zidzala nthambi za utumikiwu mdziko lonse la pansi.

Zomwe zili mbukuli ndi zotsatira za mazana a Bambo ndi a Mayi a mu utumikiwu. Mulungu akuwagwiritsa ntchito kuti afikire zikwi za anthu omwe sangathe kufikiridwa ndipo akuphunzitsa abusa ndi atumiki ena ochuluka kuti adzale matchalitchi atsopano, mdziko la Brazil, ndiye cholinga chawo.

Anthu onsewa aphunzinsidwa zabukuli, zomwe zingaphunzitsidwe mchikhalidwe chirichonse ngakhale mdziko lonse lapansi mwachidule, njira za utumikiwu, zikuphunzisa alaliki kufikira Madera amene kulibe matchalichi, kubweretsa miyoyo kwa Khristu ndi ntchito zina za tsopano.

Lero funso ndilakuti, “Kodi tingapitise bwanji mawu a Mulungu patsogolo mwachangu ndi kuyambitsa mipingo ina yatsopano?”

Yankho ndi; Kuphunzitsa atumiki mdziko lonse lapansi momwe angayambitsire ndi kutula ntchito zatsopanozi.

Pali mavuto otsiyanasiyana omwe atsogoleri amakumana nawo matsiku ano:

- 1) Kusowa masomphenya
- 2) Kusaphunzitsidwa bwino kapena mokwanira
- 3) Kusowa chidwi
- 4) Kusiyasiya mpingo kwa anthu
- 5) Kusowa mgwirizano pakati pa mipingo
- 6) Kulephera kupeza malo abwino ammizinda ikuluikulu
- 7) Kulephera kumanga kapena kugula malo chifukwa cha kukwera mtengo

Kodi tingagonjetse mavutowa? Ndizotheka, chifukwa Khristu anatigonjetsera kale. Tiyenera kuphunzitsa ziphunzitso za Baibulo, makamaka zomwe amasata mtumwi Paulo amene ali chitsanzo chabwino.

Dr. Dennis Blackmon, wofalitsa uthenga wabwino wa ku Brazil wapeza njira zoyambitsira mipingo.

1. Njira zinyi zodalilika (kukhazikitsa) mipingo

- I. Njira ya chikhalidwe pogwiritsa ntchito okhulupirira
 - a. Mpingo umafotokozera za tchitoyo moyenera
 - b. Mpingo umaitana munthu amene Sali m'busa kuyamba ntchitoyo.
 - c. Munthu oitanidwayo amapeza malo okumanirana ndi gulu latsopano limene limaphunzitsidwa Baibulo ndi kupembedzera
 - d. Mpingowo umapedza thandizo kudzera mwa a khristu opezeka m'deralo.
 - e. Okhulupilira ochepeza amayambitsa nthambi za mpingo ndi thandizo la ndalama la mpingowo.
 - f. Mpingo umapanga zitsankho zofunika ndi kuganizira zomwe awononge monga zomangira ndizolupilira anthu ogwira ntchitoyo.

2. Njira yosagwiritsa ntchito anthu okhulupilira;

Mpingo umachita chotheka mpanka ntchito yokhazikitsa mpingo itatheka. Chosiyanitsa ndi chakuti gulu la okhulupilira lomwe limapereka thandizo silimakhalapo.

3. Kugwiritsa njira zina za paderadera.

Mpingo umafotokozera ndi kutsimikiza za nthito yomwe ingabweretse zotsatira zazikulu zina mwa njirazi ndizo maphunziro a baibulo ndi kutumikira komwe sikunafikidwepo. Izi zimachitika malingana ndi mabungwe a zachuma ndi zomwe munthu amatha kupeza payenkha. Mwachitsanzo, ku Minas Gerais, mdziko la Brazil, kunasefukira madzi ndipo anthu oposera mazana angapo anasowa pokhala. Barbara Akins anapeza ndalama kuchokera ku bungwe lake ndi kuthandiza anthuwo kumanganso nyumba zawo. Woyang'anira mzindawo (Major) anapereka malo oti anthuwo amangepo ndipo malo amatchedwa kuti Beteli – Mzinda wa Mulungu. Adamanga nyumba zokwana makumi asanu ndi

awiri (70) m'chaka chanthunthu ndikuchititsanso maphunziro a baibulo. Anthu anapulumsidwa ndipo mpingo unayambitsidwa.

Pogwiritsa ntchito njirayi, ntumiki amaitanidwa kukapitiriza ntchitoyo ndipo bungwe kapena mpingo umapereka ndikutsekulira malo okumaniranapo opulumutsidwawo. Pogwiritsanso ntchito njirayi, umatha kugwiritsa ntchito zomwe utumikiwu ukugwiritsa pophunzitsa asilikaliwa ndi anthu amu mpingo kuchitira maphunzirowa mmakomo mwa anthu omwe atahndizidwa ndi njirazi kuyambitsa mpingo wina.

4. Njira yofalitsira uthenga wabwino.

- a) Mpingo umafotokozerana za malo omwe akuyenera kufikiridwa.
- b) Mbusa kapena mtsogoleri amasankha anthu okhwima nzeru kuti agwire ntchitoyo.
- c) Mbusa kapena mtsogoleri amaphunzitsa ndi kusala anthuwa moyenera. Cholinga cha bukuli ndi kuthandiza momwe mungaphunzitsire anthuwa.
- d) Anthu ophunzitsidwa aja, amayamba ntchito yatsopanoyo popangitsa maphunziro a baibulo mmakomo a anthu omwe asali akhristu (osakhulupilira).
- e) Okhulupilira atsopanowo amabweretsedwa pamodzi ndi kuyambitsa tchalitchi lomwe lili la umodzi, lodzidalira ndi lokhala pansu pa utsogoleri wa Mulungu.
- f) Atumiki amaongolera gulu la tsopanolo kupanga zitsankho pa okha ndi kuganiziranso za zomwe angaononge kuchokera ku chiyambi. Ngati gulu la okhulupilira latsopanoli likufuna kupanga lent kapena kumanga tchalitchi amalipira malo ndinso ogwira ntchito.

II. ZA BAIBULO NDI CHIKHALIDWE

Nkofunika kwambiri kusiyanitsa zokhuza baibulo ndi za cikhalidwe. Thomas Wade Akins, munthu wa ku Amereka, Mulungu anamuitana kukagwira ntchito ku Asia (Vietinam), United States (Washington DC), Africa (Zimbabwe), Brazil, kufikira lero akutsogolera misonkhano mdziko lonse lapansi.

Zinthu zokha zomwe zingasinthe chikhalidwe ndi zomwe zikutsatana ndi ziphunzitso za buku loyera (Baibulo) mwachitsanzo, m'malo ena mdziko lapansi amapereka nsembe za ana amakanda. Izi ndi zotsutsana ndi baibulo, ndiye zikatero atumiki alola kuti Mulungu absinthe chikhalidwechi polalikira uthenga wabwino wa choonadi.

Thomasi Wade Akins anazindikira izi pamene anayambitsa utumiki wake ku Washington, DC. Atabwera ku mpoto (South) kwa Vietinam, Thomas Wade anapeza kuti achinyamata ochuluka amakhala m'misewu. Iwowa amakhala kuti anachoka m'makomo mwawo, amamwa makhwala ozunguza bongo, amasunga tsitsi lalitali, amaimba nyimbo zosayenera ndi kuvala zovala za America a Chiindia ndiposo amatsutsana ndi khondo yak u Vietinam.

Palibe ngakhale mmodzi wa iwo amene amapita ku tchalitchi kuti miyoyo yawo ibwerere kwa Christu, mpingo unayenera kuwafikira. Thomas anavala zovala za Amereka a Chindia ndi kusiya tsitsi lake kuti litalike, koma samamwa mowa ngakhale makhwala odzunguza ubongo. Anatsekula malo odyera aang'ono mu mzinda wina ku England, anachotsa mipando yonse m'menemo ndipo anthu amayenera kukhala pansu, anaikanso nyale za ntundu wina, ndi ntanda waukulu womwe umawala nyale yofiira kutsogolo kwa malo odyerawa. A mpingo waz Baptist amapereka zakudya ndi zakumwa tsiku lililonse.

Tsiku lililonse, kuchokera 3:00 koloko masana mpaka 2 koloko m'mawa (m'bandakucha), Thomas, mkazi wake ndi gulu m'malo ena aliwonse mdziko lino lapansi ali ndi chikhalidwe chawochawo. Ntchito ya Ambuye

ikhazikike m'babulo komanso pa chikhalidwe chaa dziko palokha akhazikike pa miyambo ya chipembedzo. Mwachitsanz, mipingo yambiri yak u United States imayamba mapemphero la Mulungu m'mawa nthawi ya 11 koloko (11a.m). Kodi izi zitanthauza kuti mapemphero onse mdziko lonse lapansi aziyamba nthawi imeneyi?

Yankho ndi loti, ayi! Akhoza kutero ngati afuna, koma ayimbe nyimbo za mchikhalidwe chawo ndiponso agwiritse ntchito zida zawo. Mpingo ukhoza zida monga: gitala ya magetsi, Vuvuzela, ng'oma ndi zida zina.

Chenjezo! Kuyimba nyimbo sikuthokoza koma njira imodzi yothokoza. Ndinjira inanso yomfotokoza Mulungu zokhuzidwa zathu. Pachifukwa ichi ndikofunika kuti nyimbo zoimbidwa ziunike chikhalidwe cha anthu osati zimene otumikira akufuna. Ndizosatheka kukhala otumikira wachangu koma pokhapokha titamvetsa chikhalidwe cha anthuwo.

Palizikhalidwe ndi tizikhalidwe tambiri mdziko lililonse. Ndikofunika kuti mtumiki adziwe ndi kumvetsa chikhalidwe cha anthu a mdera lomwe afuna kuyamba ntchito yake. Kufunika kwinanso nkwa kuti asayesera kusintha chikhalidwe cha anthu koma atumikire, kumulora khristu kuti asithe mitima ya anthuwo.

*La utumiki amatsekula ndikuwalola achinyamata aja ndi kumwa komanso kudya kwa ulele. Achinyamata amabwera nkukala pansu ndipo Thomas ndi gulu lakenso amabwera nkumacheza nawo zokhuzana ndi moyo wawo. Izi zidapangitsa kuti ambiri asinthike ndi kubwera kwa Khristu.

III. BAIBULO NDI ULAMULIRO WAKE

Mdziko lino lapansi munthu wina aliyense amakhala ndi omulamulira ake. Dr Ralph Neighbour, Jr mu bukku lake lotchedwa **Survival kit** (Broadman Press) akufotokoza njira zinayi za ulamuliro wa chabwino ndi choipa.

Njira yoyamba:

Luntha: Apa ndipamene munthu amatsimikizika za choonadi pa iye yekha posiyanitsa pa chabwino ndi choipa, chotheka ndi chosatheka. Munthu amene akudalira zero zake akhoza kukana za zozwizwa za Yesu chifukwa kuthupi simatsimikiza. Ysaya 55:8, “Pakuti maganizo anga Sali maganizo anu ndipo njira zanga sizili ngati zanu, atero Ambuye.”

Njira yachiwiri:

Kuzindikira: Apa ndipamene munthu amatsimikizika za chabwino ndi choipa podzera ku za kumva mnthupi mwake, zokhuzika ndi zotsatira. Tsiku lina Thomas Wade adakwera galimoto (taxi) mu mzinda wa Rio de Janeiro ku Brazil ndipo adayankhula za uthenga wabwino wa Ambuye Yesu Khristu kwa woyendetsa galimotoyo. Dalaivalayo adamuziwitsa Thomas za msonkhano wa chipembezo chawo komwe m’bambo osaona anachiritsidwa kukhalanso owona. Thomas atafunsa za dzina la tchalitchiyo, dalaivalayo adamuyankha kuti sichinali chachikhristu.

Mdierekezi (satana) ali ndi mphamvu yakuchita zozwizwa, koma sangathe kupulumutsa munthu, kumpatsa ntendere weni-weni ndikumukhululukira machismo kwathunthu. Mthawi zina amachita zozwizwa ndi cholinga chofuna kunamiza (kupusitsa) anthu. Baibulo likuyankhula motere ku 2 Atesalonika 2: 9-12, ndiye amene kuza kwake kuli monga mwa machitidwe a satana, mu mphamvu yonse ndi zizindikiro ndizo zina zonama; ndinchinyengo chonse chosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza chikondi cha chowonadi sanachilandire, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo chifukwa chake Mulungu atumiza kwa iwo machitidwe a kusocheretsa, kuti akhulupilire bodza, kuti akaweruzidwe onse amene sanakhulupilire choonadi, komatu amakondwera ndi chosalungama.

Ena amanena kuti: “Ndimakhulupilira kumwa makhwala ozungua bongo ndi zakumwa zozedzeletsa chifukwa ndimamva bwino”. Munthu ameneyu akulamulidwa ndi zomwe nthupi lake likumva. Kukhala nchikhulupiliro chotere ndo kowopsa. Enanso amavti, “Ndimakhulupilira sing’annga chifukwa anandichiritsa ku nthenda yanga”. Amene amachita zozwizwa, zodabwitsa zo chuluka kupeza mwayi ndi kutchuka, pena zikhoza kukhala

kuti sizaumulungu. Tisaike chikhulupiliro chathu pza zozwizwa zomwe thupi lanthu limamva ndi nzeru zathu, m'malo mwazke tiyike chikhulupiliro chavthu mwa Yesu Khristu, amene alipo komanso malonjezo ake ali m'mawu a Mulungu.

Njira ya chitatu:

Chikhalidwe: (Zikhulupiliro). Ili linali mwa mavuto omwe Yesu anatsutsana nawo. Analimbana ndi zikhulupiliro za a Yuda zomwe amazitenga zofunikira nthawi zones osati zofunikira za moyo wa munthu. Ku mariko 3:1-6 tikuona afarisi akumuyesa Yesu:

Vesi 1 (Vesi yoyamba)- Apa tikuona zomwe zikuchititka akulowa msinagoge (Mkachisi). Nkachisimo muli anthu ochuluka ndipo kumanja mkatikati mwa gulu la anvthuwo muli munthu wopuwala dzanja.

Vesi 2 (Vesi yachiwiri)- Anthu anayamba kunong'onezana motere, “Kodi mwamuona walowayu?” ndi “Yesu”, “Kodi mwamuona wazkhalaz apoyo?” “Ndi munthu wopuwala zanja uja” “Kodi mukuganiza kuti Yesu amuchiritsa?” “Sindikudziwa potilero ndi lasabata.”

Vesi 3 (Vesi yachitatu)- Ndipo Yesu ananena ndi munthu ali ndi dzanja lopuwala Taimilira pakati. Ndipo ananena kwa iwo. Kodi nkuloledwa tsiku lla sabata kuchita zabwino, kapena zoipa? Kupulumutsa moyo kapena kupha?

Vesi 4 (Vesi yachinayi)- Koma anakahala chete. Ndipo m'mene anawaunguza ndi mkwiyo, ndi kumva chisoni chifukwa cha kuuma kwa mitima yawo.

Vesi 5 (Vesi ya chisanu)- Yesu anane kwa munthuyo, tambasula dzanja lalo. Ndipo analitambasula, ndipo linachira dzanja lake.

“Tiyamika Mulungu kuti dzanjali linachiritsidwa!” koma gulu la anthu aja sanasangalatsidwe.

Vesi 6 (Vesi ya chisanu ndi chimodzi)- Ndipo afarisi anatutluka, ndipo pomwepo anamkhalira upo ndi Aherode, wakumuononga iye, anapanga upo

wakumupha Yesu kuchokera Koyambilira kwa utumiki wake osati kumapeto chifukwa chiyani?.

1. Kodi mvuto linali chiyani pamenepa?

Yankho: Chifukwa linali tsiku la Sabata

2. Kodi mvuto linali chiyani kuchiritsa munthu tsikuli?

Yankho: Kunali kutsutsan ndi chipembezo chawo.

3. Kodi mukukhulupilira kuti Yesu ndi m'modzi mwa utatu wa Woyera komanso mwana wa Mulungu.

4. Kodi mukukhulupilira kuti Yesu ndi mwini Sabata?

5. Kodi mukukhulupilira kuti pamene Yesu anachiritsa munthu wopuwala uja pa tsiku la sabata, sanavere atate ake akumwamba?

6. Nanga mvuto linali chiyani?

Yankho: Vuto linali loti atsogoleri a chipembezo anapanga malamulo owonjezera amene Mulungu sanapange.

Kodi zimenezi ndi za tchito yanji kwa atumiki wofalitsa uthenga wabwino ndi kubzala mipingo?

M'busa Tomas Wade Akins atapita ku Brazil anapannga gulu loti lizidzala ma tchalitchi. Ambiri mwa anthu amene anawapeza a gululi anali ongokhala . Iye anawaphunzitsa momwe angachitire umboni komanso komanso mwe angayambitsire matchalitchi, anapita m'mdzinda yosiyanasiyana ndikutengera anthu ambiri kwa Khristu ndi kuyambitsanso nthambi za mpingowo. Anabzala mipingo makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zitatu (63) mudzaka ziwiri (2 years)

Komabe, Thomas Wade Akins anatsutsana ndi zikhulupiliro zamphamvu zitatu zomwe munthu anapanga zomwe zimatchinga kukula kwa mmpingo.

Chikhulupiliro choyamba

Atatengera anthu kwa Khristu , M'busa Thomas Wade adati ndi koyenera kuti atumiki aja azibatiza ndi kupereka mgonero kwa anthu omwe atembenuka mtima, koma ena mwa abusa ananena kuti sizingatheke chifukwa sanadzodzedwe (sanasankhidwe).

Thomas anafunsa, “ndipati pamene Baibulo likuphunzitsa zimenezi” ndipo yankho linali loti Baibulo silimaphunzitsa izi koma akutenngera zikhulupiliro ndi malamulo awo.

Ndondomeko yakasankhidwe kamasiku ano sili mbuku loyera (Baibulo) ngakhale kale kunalibe zimenezi. Pakuti mawu oti kudzodza atanthauza kusankhidwa, kutumidwa kugwira ntchito ya Mulungu. Pa Yohane 15:16, Yesu “asankha” (kudzodza) ophunzira ake . Inu simunandisankhe ine koma ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakitani kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso, ndikuti chipatso chanu chikhale , kuti chimene chilichonse mukapempha atate m’dzina langa akakupatsani inu.

Pa machitidwe atumwi 14:23. Paulo akuyankhula za akulu osankhidwa. “Paulo ndi Banaba anawaikira akulu mosankha mu mpingo, ndi kupemphera pamodzi ndi kusala kudya, anaikiza iwo kwa Ambuye amene anamukhulupilirayo.”

Kudzodza inali ntchito ya Mulungu osati ya munthu Mulungu amalozha amasankha ndi kupatula atsogoleri mu ndondomeko za kusankha anthu okatumikira zikupyora za ‘mbaibulo mmaiko ena amafuna kuti munthu achite maphunziro a baibulo kapena a nsembe asanapatulidwe. Kodi ndi seminal iti yomwe Yesu anapita? Ndipo di seminare iti yomwe Petro, Paulo ndi Yohane adapita? Ndindani yemwe adabatiza mtumwi Paulo, ndi abusa kapena atumiki? Ndi anthu ochulukira motani womwe Yesu adawabatiza?

Kodi ganizo loti okha azibatiza ndi kudyetsa mgonero lidachoka kuti? Mu mbiri ya mpingo, timachita za m’chipangano chakale mmene wansembe amawachitira anthu china chilichonse. Mbali ina ndi mpingo wakatolika.

Chikhulupiliro cha chiwiri

Tiyenera kukoza nthambizi kuti zikhale mipingo, anatero Tomasi koma ena adanena kuti sizingatheke kufikira atamaga kapena kukhala ndi malo awo. Mbusa Tomasi adafunsanso kuti ndi pati pamene baibulo limaphunzitsa izi:

Ndipo anthuwo adayankha kuti Baibulo silimaphunzitsa koma ndi chikhulupiliro chathu.

Chikhulupiliro chachitatu- Mu dziko lina abusa adanena kuti lamulo la mpingo silingalole kukhazikitsa tchalitchi pokhapokha atakwana anthu makumi asanu (50). M’busa Tomasi adattinso, “Kodi pati pamene baibulo linaphunzitsa zimenezi?” Nkuyankha kwawo adati silimaphunzitsa koma chikhulupiliro chawo.

Nthawi zambiri miyambo (zikhaliidwe) kapena zikhulupiliro zathu ndi za mphamvu kwambiri kuposa mawu a Mulungu ndipo izi ndi zomwe Khristu adakumana nazo. Ngati tifuna tiwone ufumu wa Mulungu ukukula ndi mipingo yatsopano ikubzalidwa tiyenera kutsatira baibulo ndi mawu a Mulungu osati malamulo opangidwa ndi munthu. Ngatinso tikufuna kuona kabzalidwe ka mipingo kakupita patsogolo tiyenera kupereka mphamvu kwa atumiki anthu ku ntchito yomwe Mulungu adawaitana kukachita ndi kutsatira ziphunzitso za mbaibulo pa zakuti mpingo ndi chiyani.

Pamene taika miyambo pamwamba pa mawu a Mulungu mawuwo amakhala ngati opanda ntchito. Yesu akuyankhula ku Mateyu 15 v 6-9 kuti iyeyo sadzaleka kulemekeza atate wake. Ndipo inu mupeputsa mawu a Mulungu chifukwa cha miyambo yanu. Onyenga inu: Yesaya ananenera bwino za inu, ndikuti, athu awa andilemekeza ine ndi milomo yao; koma mtima wawo uli kutali ndi ine. Koma andilambira ine kwachabe ndikuphunzitsa ziphunzitso, malangizo a anthu.

Chachinayi. **Malemba:** Mawu a Mulungu ndiwo amene ali ndi ulamuliro. Mulungu amavumbulutsa zinsinsi kudzera mawu ake, ndipo amapatsa nzeru yotheratu.

Ku Yoyane 8: 32, Yesu akuyankhula kuti “muzadziwa choonadi ndipo choonadi chizakumasulani”.

Ku Yesaya 40 v8 mawu a kuti, udzu unyala, duwa lifota, koma mawu a Mulungu adzakhala nthawi zachikhalire.

Masalimo 119:105 akuti “mawu anu ndiwo nyali ya kumapazi anga ndi kuunika kwa panjira yanga.”

Masalimo 119:160 ikulankhula kuti, “chiwerengero cha mawu anu ndicho choonadi, ndi maweruzo anu olungama onse akhala kosatha.”

Ku Yohane 14,6, Yesu akuyankha kuti, ine ndine njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu odza kwa atate, koma mwa ine.

Kodi choonadi ndi chiyani?

- A. Yesu khristu
- B. Mau a Mulungu

IV. ANGAYAMBITSE KUKHALA OTUMIKIRA NDANI?

Mtumwi Paulo adatsata njira izi pobzala mipingo.

1. Iye analowa mu mzinda
 - Ulendo wake woyamba- zomwe zikupezeka pa *machitidwe atumwi 13v 5, 6, 14; 14 v1, 6, 24, 25*
 - Ulendo wake wachiwiri- zomwe zili pa *machitidwe atumwi: 16 v 2; 17 v 1, 10,15; 18:1-19.*
 - Ulendo wake wachitatu- *machitidwe a tumwi 19 v1, 20:2*
2. Analalikira (Anafalitsa) uthenga wabwino: pa *machitidwe a tumwi 14 v 3, 7, 21, 25.*
3. Anaitengera miyoyo yambiri kwa khristu:-zomwe ziri pa *machitidwe atumwi 14 v 1, 21, 19 v 8.*
4. Adaphunzitsa okhulupirila omwe omwe anali atsopano;- monga pa *machitidwe atumwi 14 v 27, 15 v 36, 18 v 23, 19:9,10.*
5. Anawaphunzitsa nndi kuwapatsa maluso autsogoleri. Monga pa *machitidwe atumwi 14 v 27, 15 v 36, 16 v 5, 20 v 20.*

6. Anakhazikitsa mipingo ndi kusankha atsogoleri kuti apitirize utsogoleri m'mipingo: monga pa *machitidwe atumwi 14 v 23, 20 v 17,28*.

7. Paulo anachoka mu mzindawo ndikupita ku mzinda wina: pa *machitidwe atumwi 20 v 36-38*.

Izi ndi zomwe omwe akuyambitsa kutumikira angachite pamene akupita kukatumikira ndi kuyambitsa mipingo ina yatsopano.

Funso kwa ife ndi lakuti, “anngayam bitse kukhala otumikira ndani?” kuti tiyankhe funso tiyenera kuwerenga *Aefenso 4 v 11-12*. Mu n dimeyi, pali ntchito zomwe mpingo umagwira.

Ntchito yoyamba ndi kukhala “mtumwi.” Pali mitundu iwiri ya atumwi otsatira yesu oyamba anali atumwi ndipo Paulo anali mtumwi. Mawu oti “atumwi” atanthauza kuti “wotumidwa.”

Ntchhito yachiwiri ndi kukhala “aneneri.” Aneneri anali alaliki ndipo mawu oti “mneneri” akupezeka kokwana mazana awiri ndi makumi anayi ndi mphambu ziwiri (242 times) mu baibulo ku Deuteronomo 18 v 18 akulongosola za ntchito yawo yeniyeni. “Ndizawaukitsira mneneri wa pakati pa abale awo, wonga iwe,” ndipo ndidzapatsa mawu anga mkamwa mwache, ndipo adzanena nawo zonse ndimuuzazi.

Ena mwa aneneri m'chipangano chakale anali *Aroni Eksodo 7:1*, Mose, Elisa, Yesaya, Yeremia, Daniel ndi ena ambiri. Mkazi wa Yesaya analinso mneneri. (Yesaya 8 v 3). Mchipangano chatsopano, ena mwa anai (anamwalira) a Filipino. (*Machitidwe 21 v 9*).

Gulu lachitatu ndilo la “alaliki”. Anthu zamenewa ndi omwe amafalitsa uthenga wabwino wa Yesu Khristu ndi cholinga chofuna kupindula miyoyo yotaika. (Awa ndi amene amatchedwa oyambitsa mu utumiki umenewu). Filipino ntumiki komanso mlaliki. *Machitidwe 21 v 8* mawu akuti, “Ndipo m'mawa wache tinachoka, tinafika ku Kaisareya ndipo mmene tinalowa nyumba mwa Filipino mlaliki, mmodzi wa asanu ndi awiri aja, tinakhala naye. Iye anali munthu amene analalikira uthenga wabwino kwa anthu otaika ndi kuwabatiza. Pa *machitidwe 8 v 12* mawu akuti “koma pamene anakhulupilira Filipino wakulalikira uthenga wabwino wa ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Khristu, anabatizidwa, amuna ndi akazi.” M'dziko lonse lapansi, lero tili

ndi abambo ndi amayi omwe akukwaniritsa ntchito ya atumiki poyamba mipingo yatsopano.

Utumiki wachinayi ndi okhala “Mphunzitsi”- “m’busa” Abusa ndi anthu omwe ali ofunika kuyamba kuphunzitsidwa. Iwo ndiatsogoleri muuzimu , atchito amene amatsogolera anthu mu njira za Mulungu. Iye akuyenera kukhala nayo mphatso yakukhala mphunzitsi komanso wosula (wopereka luso kwa ena).

Mkhristu payekha amene ali mwa khristu amalandira mphatso ya uzimu pamene woyera walowa mu mtima mwake atatembenuka mtima. Ku *1 Petro 4 v 10* mawu akuti “monga yense walandira mphatso yakukhala mlaliki’.

Angayambitse ndani? Angalalikire, kutumikira ndi kubzala mmipingo ndani? Kodi m’busa akhoza kukhala oyambitsa, kapena mtsogoleri? Kapena woxweruza milandu?, kapena mphunzitsi.

Wina aliyense akhoza kuyambitsa makamaka amene akumva mayitanidwe akukhala mlaliki ndi kukwaniritsa zomwe Baibulo limafu, koma zoyeneraza ndi ziti kuti munthu akhale oyambitsa posayang’anira kuti - munthuyo ndi m’busa kapena mdindo? Akuyenera;

1. Akhale opulumutsidwa (*Machitidwe 9*).
2. Amve maitanidwe ake (*Agalatiya 1 v 15-16*)
3. Akhale odzadzidwa ndi mzimu woyera (*Agalatiya 5 v 16, Aefeso 5 v 18, ndi Machitidwe 13 v 9*)
4. Adziwe kugwiritsa ntchito mawu a Mulungu (*2 Timoteo 2 v 15*)
5. Akhale ndi khumbo lomusangalatsa ndi kumvera Mulungu (*1 Atesalonika 2:4*)
6. Akonde otembenuka mtima ndikusamalira iwo (*1 Atesalonika 2 v 7-12, Tito 1 v 9*)
7. Akhale odziwa kupemphera (*1 Atesalonika 1 v 2, Akolose 4 v 2-6*)
8. Akhale m’moyo woyeretsedwa (*1 Timoteo 5 v 22, Tito 1; 7 v 8*)
9. Akhale olimba mchikhulupiliro (*Tito 1:9*)

Tingatengere bwanji miyoyo yochuluka kwa khristu ndi kuyamba mpingo m'mizinda ndi m'midzi ngati sitikuphunzitsa anthu omwe ali ndi mphatso yakukhala alaliki. Abusa sangathe kufikira dziko lonse la pansi pa za khristu chifukwa ndi ochepa. Annthu a Mulungu ayenera kuphunzitsidwa ntchitoyo.

Ngati alaliki ophunzitsawa ataphunzitse gulu lalikulu la zanthu ene anagakwaniritse zomwe Baibulo likufuna, tikwaniritsa cholinga choyambitsa matchalitchi m'mizinda, m'malo oyandikira ndi mmidzi pa dziko lonse la pansi.

Woyambitsa utumikiwu ndani? Ndi amene waitanidwa ndi mzimu woyera kuti afalitse uthenga wabwino wa Khristu ndi kuyambitsa mipingo yatsopano.

V. NTCHITO YA ALALIKI OYAMBITSA UTUMIKI

Ntchito yofunika ya m'busa, mlalikindi mtsogoleri wa muuzimu amene amapulumsa anthu ake.

Pa Aefeso 4 v 11-12 akufotokoza momveka bwino za ntchito yofunika ya m'busa. Baibulo likuyankhula kuti MMulungu anatipatsa abusa otiphunzitsawa kuti tikozekeretse ku ntchito yake yakumanga thupi la Khristu. "Kusula" kutanthauza kuphunzitsa anthu kuti ntchito igwirike mu utumiki, osati kudziwa ziphunzitso zokha.

Mau ena, m'busa kapena mtsogoleri, ntchito yake yeniyeni ndi kuphunzitsa ndi kusula anthu kuti atumikire ntchito yomwe Mulungu anawapatsa.

Kuti timvetse bwino ntchito ya m'busa, tiganizire gulu losewera mpira wa miyendo. Timu ya mpira wa miyendo imakhala ndi osewera komanso owapatsa malangizo a mu mpira. Kodi owapatsa malangizo amasewera mpira kapena amangowaphunzitsa momwe angasewerere?

Yankho ndi loti amawaphunzitsa momwe angasewerere.

M'busa kapena mtsogoleri pa mpingo kapena mtchalitchi sikuchita utumiki koma kuphunzitsa anthu momwe angatumikire. Ayenera kuwaphunzitsa chilichonse momwe iye amachitira monga momwe angachitire umboni, angalalikire uthenga, angabatizire momwe angadyetsere mgonero ndi china chilichonse.

Tomasi Wade adagwirapo ntchito ngati Mthandizi wopala matabwa. Opala matabwa anapanga gulu la umodzi. Tsiku lina mpala matabwa ndi Tomasi amagwira m'mwamba pamakwelero. Kalipentalyu anali onenepa ndipo kutengera pamakwelero pomwe analisakanatha kudulathabwa. Anayang'anayang'ana kuti aone ngati wina amamuona ndipo anati, "Tomasi ukhoza kudula thabwa." Tomasi anayankha nati ndizotheka, palibe vuto. Koma chifukwa chiyani amayang'ana motero motero?" kalipentala uja analongosola kuti chifukwa chakuti Tomasi sanali mu gwirizano wa makalipentala sanali oloedwa kudula matabwa kapena kukhoma misomali.

Masiku ano, m'maiko ambiri, m'mautumiki a lero, abusa ali mu gwirizano. Abusa angathe kubatiza, kuchititsa mgonero wa Ambuye ndi zina koma atsogoleri ena sangathe kutero. Koma mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti tonse muyesetse kupeza.

CHACHIWIRI: ANAPHUNZITSA OPHUNZIRA AKE

Mbali ina ya bukhuli ikuphunzitsani momwe mungaphunzitsire gulu lanu.

CHACHITATU: ANAWATUMA OPHUNZIRAWO

Palinjira zambiri zomwe mungagwiritse ntchito potuma gulu lanulo ndi cholinga choti mpingo ukule komanso mipingo ibzalidwe. Pali njira zitatu momwe tingawiritsire ntchito gulu la anthu khumi ndi awiriwa (12)

- Gawani dera lanu m'magawo khumi ndi awiri ndipo mupange aliyense wa gululi kukhala mtsogoleri dera lakelake. Iwowa ndi amene atakhudzike kutumikira kumaderawo.
- Tumani (atsogoleriwa) kumizinda, kumidzi ndi kumalooyandikira osiyanasiyanaokwana khumi ndi awirikuti akayambe ntchito zina zatsoppano.
- Mbali ina yakuwafikira mosavuta ndi kuwatuma mdera lawo lomwe kuti alalikire ndi cholinga chokulitsa mpingo ndi kuwatumanso ena m'mmalo oyandikira, m'mizinda ikuluikulu ndi ing'onoing'ono kapena m'midzi kuti akayambitse ntchito zatsopanozi. (Mtsogoleri aliyense payekha munthawi apanga kagulu kake ka anthu awiri kapenna kupitilira apo n di

kuwaphunzitsa zomwe iye adaphunzira. Gulu la mtsogoleriyu likhoza kuyamba kulalikira dera lawo ndi kuyambitsa ntchito zatsopano.) ndife atumiki, 1 Petro 2:4 mawu akuti, “amene pakudza kwa Iye, mxwala moyo wokanidwatu ndi anthu, koma ndi Mulungu wosankhika waulemu.” 1 Petro 2 v 9 mawu akuti, “koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu xwoyera mtima, anthu amwini wache...”

Wina aliyense okhulupilira mwa Khristu ndi wansembe, mtumiki ndipo palibe migwirizanno mu ufumu wa Mulungu. Abusa ayenera kuunikira nt chito yawo ngati akapolo a Mulungu, atsogoleri auzimu amene ayenera kugwira nt chito mbali zonse.

Yesuanatha zaka z tatu akuphunzitsa ophunzira ake, ndipo ndi chitsanzo changwiro ku dziko lonse lapansi. Chiphunzitso chokhazikika chomwe amagwiritsa nthito “chakuchulukitsa” chimene Iye amachita ndi zomwe ife tiyenera kupanga. Kodi Yesu anachita chiyani?

Yesu anali ndi mautumiki awiri:

1. Amachita utumiki wapoyera. Analalikira kwa anthu ochuluka
2. Amachitanso utumiki wachibisira. Uwu ndi utumiki womwe unabweretsa zotsatira za mphamvu ku dziko lapansi.

Mu utumiki wake wachinsinsiwu anachita zithu z tatu

CHOYAMBA : ANAPANGA GULU LA OPHUNZIRA

Gululi linapangidwa ndi anthu khumi ndi awiri (12) sizikutanthauza kuti muyambe utumiki ndi anthu khumi ndi awiri (12). Mukhoza kuyamba ndi munthu m'modzi ngati zingatheke. Ngati palibe ngakhale m'modzi mtsogoleri oyambitsa utumiki (the pioneer Evangelist leader) nayenso akhonza kuyambitsa gulu lotumkira la anthu okhazikika ndi kuwaphunzitsa kulalikira, kutuikira ndikudzala mipingo. Bukhuli likuphunzitsani momwe mungachitire izi koma choyamba ndi kukhalazikitsa gulu lanu. Chofunika ndi chii muyenra kupindula miyoyo ingapo ngati mulibe wokhulupilira ngakhale m'modzi woti muphunzitse.

Mutatha kupindulira miyoyo kwa khristu, mwayenera kuitumikira ndi kupanga gulu la otumikira ameme mungawaphunzitse kuti akhale otumikira oyambitsa ndi

kuwatuma. Gulu la otumikirawa ndi limene likuchedwa oyambitsa m'bukhuli. Cholinga ndi choti wina aliyense wa mgulu akhale mtsogoleri oyambitsa kulalikira ndi kupanga gulu lake la otumikira, iyi ndi njira yakuchulukitsa.

Minapanga gulu lanu m'nira ziwiri

Njira yoyamba – Ndikuulutsa muli pagome kuti muyambitsa gulu la otumikira ndi kuitana aliyense kutengapo mbali. Mulungu adzadzutsa anthu ena omwe simunawasankhe. Mwachitsanzo: kodi kodi mukadasankha mateyu, wokhometsa msonkho kukhala mtumiki?

Njira yachiwiri – Ndikuchita zachinsinsi, pemphereni kwa mulungu ndi kumupempha amene akuyenera kupezeka mgulu lanu, kenako mupite kwa anthuwo mwachinsisi kuti akhale gulu lotumikiralo. Muwadzitse kuti midzikumana ka modzi pa mulungu, muwaphunzitse ndi kuwatuma kuti akagwire ntchito ndi cholinga chofuna kubweretsa anthu kwa yesu khristu.

Mtsogoleri oyambitsa utumiki ali ndi ntchito ziwiri zofunikira.

Ntchito yofunikitra yoyamba – Kuphunzitsa otumikira oyambawa m'modzi modzi kapena m'magulu ang'onoang'ono Abusa onso kapena ndi atsogoleri apange gulu lawo . muyenera kukhala ndi anthu khumi ndi awiri mgulu lanu. Awa ndi amene munawaphunzitse kuti akhale atumiki. Simungakhazikitsa guluri ngati mulibe anthu, choyamba mupeze anthu ndi kuwaphunzitsa. Mukatero muyenera kumakumana ndu gulu lanu sabata iliyonse ndi kumapemphera, kufotoza zochitika zofunikira ndi kuphunzitsana.

Dr. Waylon Moore, mu bukhu lake lochedwa “multiplying disciples” anafokonza izi:-

- a) Kutumikira ndi njira yabwino yomwe imathandiza kukhala ndi utumiki wopanda malire.
- b) Kutumikira ndi njira yosavuta.
- c) Kutumikira ndi njira ya change ndi yotetezeka pakudindikiritsa ena kulalika za thupi la khristu.

- d) Kutumikira kumatenga nthawi yayitali kuti konetse zipatso zake poyerekezara ndi mautumiki ena.
- e) Kutumikira kumabweretsa anthu okhazikika pa za khristu komanso ophunzitsidwawo bwino za mau a mulungu.

Ntchito yofunika yachiwiri – ndikuphitiriza kukumana ndi atumikirawo pa sabata liyomse. Atsogoleri oyambitsawa akhale ndi otumikirawo kwa nthawi yokwana ola limodzi pa sabata.

Zoyenera kuchita mmisonkhano imeneyi.

- a) Atsogoleri oyambitsawo ayambe ndi pemphero, tili mu nhondo ya uzimu ndiye chitetezo chathi ndi pemphero.
- b) Mufunse otumikir aliyense payekha kugawana zigonjetso zomwe wazona msabatayo.
- c) Afunsidwensoko kufotokoza za mavuto omwe akumana nawo msabatayo ndi kuwaunira.
- d) Apatsidwe uphungu pa vuto lilionse lomwe anafotokoza.
- e) Aphunzitsidwe pogwiritsa ntchito mbali ya bukhuli. Mwachisanzo muwerengetso pa mutu oti “ungapereke bwanji umboni” kapena utumiki cholinga ndikuona momwe angabweretsere anthu kwa ambuye zingakhalenso zofunikira kwambiri mutaunikanso mbali zina monga “pemphero” “njira zopanga chindunji” kapenenso ina ndi ya momwe tingaphunzitsire atsogoleri. Nthawiyi mutha kuphunzitsanso ogwira ntchito.
- f) Aphunzitse zoyenera pa utumiki monga momwe angalembere uthenga, momwe angaperekere uphungu ndi zina ndi udindo wa atsogoleri oyambitsawa kuphunziotsa otumikira moyenera.
- g) Auzidwe zoyenera zones ndi kumaliza ndi pemphero.

Mtsogoleri otumikirayo ayenera azipangitsa misonkhano kamodzi pa mwezi kapena patatha miyezi iwiri.

Izi ndi zomwe mtumwi Paulo anali kuchita. Ndizofunikira kwambiri kuti mtsogoleri aziyendera otumikira ndi kupitiliza kupanga nawo misonkhano.

Ntchito yeniyeni ya mbusa kapena mtsogoleri ndi yotani?

Kodi midzadzipereka kukhazikitsa gulu, utumiki ndi kuwaphunzitsa mwa luso.

VI. GULU LOTUMIKIRA NDI KULALIKIRA

Ntchito ya mtsogoleri woyambitsayu ndi kuphunzitsa anthu a mtchalichi yake kukwaniritsa ntchito yawo. Pachalichi ilionse, mulungu anaika amene ali ndi mphatso ya kulalikira ndi kudzala mpingo yatsopano. Mtsogoleri yoyambitsayu ali ndi kuthekera kozindikira anthu a mphatso zoterezi. Ntchito yinaso ndi ndi kuphunzitsa abambo ndi amayi paokhaokha pogwiritsa ntchito buku la “Pioneer Evangelism” ndi mabuku ena abwino. Gula la anthu omwe akutumikirawa liziwike ngati alaliki ndi mpingo, ndipo mpingowo udzakhala ukuwapempherera, kuwathandiza ndi kuwatuma kukayambitsa ntchito zatsopano.

Zolinga ndi zokhumba za gulu lotumikira ndi kulalikira.

1. Kupindulira miyoyo kwa ambuye yesu.
2. Kubatiza anthu omwe atembenuka mtima.
3. Kuatsa ndi kuwatumikira omwe atembenuka mtima
4. Muphunzitse atsogoleri kumene ntchito ikuyamba kumene. (mulungu adzadzutsa atsogoleri atsopano omwe adzafunike kuphunzitsidwa ndi atsogoleri oyambawo)
5. Khazikitsani mpingo omwe ungate kukhazikika, wogwirizana ndi wodzidalira pansu pa utsogoleri wa mzimu woyera wa mulungu.
6. Kuyamba kuchulukitsa ntchito zina zatsopano. Aliyense oyambitsayo adzakhala mtsogoleri woyambitsa kulalikira ndi kudzala mipingo pakupanga gulu ndi kuyamba ntchito zatsopano.
7. Iyi ndi njira yokhazikitsira kadzalidwe ka mpingo.

VII. NJIRA ZISANU NDI ZINAYI (9) ZOKHAZIKIKA ZOYAMBITSIRA MIPINGO YABWINO

Mu bukhu lake, Donald Mcgravran, understanding church growth. Ndi Howard snyder mu bukhu lake lotchedwa orientations for starting urban churches, anafotokozamo njira zomwe zingapindule podzala mpingo.

Njirazi zimagwira ntchito dziko lililonse mu dziko limnse lapansi. Zimagwira ntchito m'mizinda ikuluikulu ndi ing'onoing'ono

A. Azindikire anthu omwe ali ndi mphatso ya uzimu yoyambitsa ntchito zatsopano.

Mpingo uliwonse uli ndi anthu oyera mtima ndi alaliki omwe ali ndi mphatso yakulalikira ndi kuyambitsa ntchito zatsopano. Monga mawu akulankhula ku *Aefeso 4 v 11-12*. Ntchito ya atsogoleri oyambitsawa, abusa kapena anthu oyera ndi kukonzekera oyerawa ku ntchito ya utumiki. Aroma 12 v 6-8, 1Akilinto 12 v 4-11

B. Kukhazikitsa utsogoleri wa oyera mtima.

Kukhazikitsa utsogoleri wa oyera mtima ndi madziko akulu oyambitsa tchalichi/mpingo kudera komwe kulibe mpingo. Kupanda kulimbika kwa oyera mtima sipadakakhala utumiki odzozedwa okwanira kuti akwaniritse cholingachi. Ntchito ya atsigoeriwa ndi kukonzekeretsa anthu oyerawa ku ntchito ya utumiki. Aefenso 4 v 11-12 mawu akuri, “Ndipo iye anapatsa ena akhale atumwi, ndi ena aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena abisa, ndi ena aphunzitsi kuti okonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la khristu.”

Mbusa wa mpingo wina anati “ngati ndingalole oyerawa kubatiza ndi zina. “ine ndi chita chiyani?” Mbusayu amanvetsa mochedwa pa ntchito ziwiri zikuluzikulu zofunikira:

A. Aphunzitse anthu oyerawa kukhala alaliki.

Alaliki amenewa amadzakhala okhwima mu uzimu ndipo ndi amene amakhala otumikira ndi kudzala mipingo.

B. Aphunzitse atsogoleri kapena alaliki omwe azatenge ntchito ya utsogoleriwa mwachangu.

Ndizofunika kuti atsogoleri amenewa aphunzitsidwe mu zikhulupiriro za m’baibulo monga kukhala ndi nthawi ya chete, momwe angakuzire chikhulupiriro chawo ndi momwe angatengere mbali ku utsogoleri wa mpingo.

Paulo analalikira ku atesalonika kwa masabata ochepa koma anasiya mpingo wokhazikika mu nzindawo ndipo anasiya m' manja mwa anthu oyera mtima a kutesalonika.

Anakhala ku Aefenso kwa zaka ziwiri akuphunzitsa msukulu ya Turano *machitidwe atumwi 19 v 9*. Kodi zotsatira zinali zotani? Anthu onse mchigawo cha m'Asiya anamva mau a mulungu. *machitidwe atumwi 19 v 10,20*. Paulo sanangochita izi payekha, iye nthawi zonse amaperaka mwambo kwa oyera mtima kuti akwaniritse mawu a mulungu.

Ku 2 Timoteyo 2 v 2 mawu akuti, “*koma zimene mwazimva kwa ine mwa mboni zambiri zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika amene adzadziwa kuphunzitsa enanso.*” Ndime imeneyi ikulongosola momveka bwino chinsisi cha kupambanira pa moyo wa Paulo. Amakwaniritsa ulamuliro wa yesu momwe analamula ife kuti “tipange utumiki” Paulo anaphunzitsa ena kuti aphunzitse anzawo.

C. Tikhale omvetsa mokhazikika zomwe baibulo likunena za chikhalidwe cha mpingo.

Ndizosatheka kuyamba chinthu chomwe sukuchidziwa. Kodi mpingo/tchalichi ndi chiyani? Mpino ndi gulu la akhristu abatizidwa amene ali mu gwirizano kukwaniritsa zolinga monga izi: *machitidwe 2 v 4-47*

- i. Kupembezera
- ii. Kularikira
- iii. Kutumikira
- iv. Kapolo wamautumiki
- v. Kusunkhana pamobzi

Kodi chikhalidwe cha mpingo ndi chiyani? Kodi zizindikiro zake ndi ziti?

- a) Ukhale ogwirizana pansi poutsogoleri wa mzimu woyera.
- b) Ukhale wolimbikitsa kapena wothandiza kupyolera mu utsogoleri wa mulungu.
- c) Ukhale wodzidalira pansi pa utsogoleri wa mulungu.

d) Adziwe madea omwe angalandire mawu mwachangu.

Njira inodzi yodziwira Madera omwe angalandire mawuwa mwachangu ndi kuona, komwe zinthu zambiri zomwe anthu amazikonda zimachitikachitika. M'madara amenewa, olalikira oyambitsawa atha kupeza omwe angaulandire uthenga mwachangu ndi mosavuta.

Njira ina yozindikira anthu achangu pakupeza anthu omwe akufunitsitsa mulungu chifukwa cha vuo lina lake. Izi zikhonza kuchititsa aliyense posatengera gulu limene ali, nthawi zambiri anthu olemera amakhala mu mkangano ngi ana awo chifukwa cha makhwala ozunguza bongo ngi mavuto ena. Uthenga wabwino uli ndi yankho pa zotsowa za anthu osewa pa dziko lino lapansi. Ntchito athu ndi kupeza anthu ngati amenewa ndi kkugawana nawo za khristu.

e) Ikani chikhulupiriro chanu mwa khristu kwatunthu palibe chofinikira kwambiri ngati chikhulupiriro. Atumwi anali ndimauthenga akulapa kumuvomereza yesu ngati chipulumutso. Anafalitsa uthenga ndi mtima wonse kotero anafikira dziko lonse la pansu. Lero tiyenera kuchita chimodzimidzi. Pa masalimo 126 v 6 akui “iye amene ayendayenda nalira ponyamula mbeu yakufetsa, adzabweranso ndithu ndi kufetsa mokondwera, ali kuyamba mitolo yake.”Ngati simukolola mu utumiki wanu mwina nkutheka kuti simukufesa moyenera. Mudzifunse kuti ndi anthu angati omwe amva umboni wanu wokhunza za khristu sabata yatha ndipo ndi angatinso omwe aitanibwa ku chiulumutso. Ulaliki kapena fufalisa uthenga wa bwino sikokwanira. Payenera kukhala ulaliki wipatsa chidwi. Ulaliki woterewu ndi pamene munthu amapatsidwa mpata wovomereza ndi kupereka moyo wake kwa yesu khristu kuti akhale mbuye ndi mpulumutsi wake. Ndiliti lomwe munapemphera kapena kulilira chipulumutso cha omwe adataika?

f) Kilimbikitsa kiyambitsa mpingo kunyumba . Paulo analalikira uthenga kwa Ayuda ndi Achikunja. Atatha kulalikira uthengawabwino mmzinda, anthu otembenuka mtima anasonkhana pamodzi. Nthawi imeneyi zambiri zambiri amasonkhana mwa akhristu asopano . nthawi zina amagwiritsa ntchito malo ngati nyumba kapena pasukulu.

Awandi ena mwa malo amene amagwiritsira ntchito

- i. Machitidwe 16 v 40 kunyumba kwa Lidia-Filipi
- ii. Machitidwe 17 v 5,6 ku nyumba kwa Yason-Atesalonika
- iii. Machitidwe 18 v 7 ku nyumba kwa Tito Yusto
- iv. Machitidwe 19 v 9 ku sukulu ta Turona-Efeso
- v. Machitidwe 20 v 20 Paulo anaphunzitsa pa mabwalo ndiponso kupita nyumba ndi nyumba.

Masiku ano, makamaka m'midzinda yathu ikuluikulu, ndi kofunika kuti mipingo idziyambira makomo chifukwa cha kukwera kwa zinthu. Akhristu kulikonse amasowekera kopembezero ndi kusonkhana pamodzi wina ndi mzako. Izi sizisowekera nyumba kapena malo opembedzeramo, makamaka poyambilira. Pogwiritsa ntchito makono mpingo utha kukhala popanda kulipilira nyumba.

Vuto limabwera polipia kapena kugula ndi mtengo wa chithandizo. M'midzinda yaying'onoing'ono malo ndi asavita kuwapeza pamene m'mizinda yikuluikulu zimakhala sosiyana pa chifukwa ichi, ndi kwabwino kugwiritsa ntchito mmakomo ndi m'malo ena poyambirira.

Tazindiira kuti kkumvana kumachulikira pamene tchalichi lili malo amene alendo amatenga mbali pa zochitika popanda mantha, komanso pogwiritsa ntchito njirayi zaonetsanso kuti zosavuta kufikira anthu oyandikira ndi mizinda.

Vuto lomwe limakhalapo anthu akamapemphera makomo ndi lakuti anthu ena amaona ngati ndi kumene akhonza kuchita izi ndi cholingaa chofuna kupirira kapena kugula nyumba.

Cholinga chathu nfi kokonzeretsa ntchito zotsoapano kuti zither kupasa zoyenera zowa pasadalira thandizo lochokera kunja

Phinzitsani okhurupirira atsopano, ntchito zatsopano kuti akhale ndi masomphenya akuyamba ntchito zochulukira.

VIII. MIFUNGULO YOKWANA ISANU NDI UMODZI MWA MIPINGO YOME YANGOYAMBA KUTI IKULE

Pamene mpingo wayambitsidwa, kodi ungakudzidwe bwanji? Nkhani yokhunza izi yalembedwa m'mabuku ambiri komanso maphunziro achitika.

Koma kuti mpingo ukule pali zinthu zokwana zitsanu ndi chimodzi zofinika kwanbiri. Monga izi:-

1. UTUMIKI WA PEMPHERO

Mpingo umafuna pemphero lokhazikika. Abusa kapena atsogoleri asamangowawuza anthu kuti adzipemphera koma kuti ayenera kuwaphunzitsa omwe angapempherere. Vuto lomwe lili ndi akhristu ambiri ndi loti sadziwa kukhala ndi nthawi ya paokha ndi mulungu wawo. Pali maganizo monga awa:-

- Gwiritsani ntchito gawo la bukhuli pa moyo wanu.
- Phunzirani kumva mawu a “mulungu” ndi kupembedzera tsiku limodzi pa sabata. Ndikofunika kupanga mndandanda wa zopembedzera ndi zina.
- Phunzitsani anthu momwe angapemphelere ndipo agwiritse ntchito pemphero pa moyo wawo. Ichi ndi chifukwa chake akhristu ambiri amakhala ndi nthawi yochepa mpemphero ngakhale amamva mauthenga akufunukira kwa pemphero.
- Pangani magulu opephera mmakomo. Mchitidwe wopemphera suletsedwa
- Tsilizani mapemphero muli chigwadire m’magulu ang’onoang’ono ichi ndi chofunika kuti mpingo ukhale wa pemphero.
- Pangani mwambo wolambira wosangalatsa omwe utapereke chimwemwe kwa okhulupirirawo.

Tikafika mchifupi ndi mulungu, timasendera mowona mtima. Ku Mateyu 6 v 9-13, mulungu akutiphunzitsa kuti tikfike ku mpando wake tikulambira. Kulambira ndiko yankho lathu lalikulu ndi kukoma kwa mulungu. Timakhala ndi chidwi ndi maina onse a mulungu pa chimene iyeyo ali (kuthokoza ndilo yankho lalikulu pa chimene mulungu wahita) iye ndiye wamuyaya, analipo, alipo adzakhalapo. Iye ndi wamkulu wamphamvu zones, wopereka ndi wochoza.

Pali maina ochuluka amene tingamuchulire mulungu mkuthikoza ndi kumukonda mulungu chimene ali izi ndi zomwe zimachitika mu mtima mwa munthu ndipo zingasonyezedwe nu njira zosiyanasiyana.

- Osapereka chiphinjo cha zinthu kwa anthu. Ndi zinthu zabwino kuti gulu la akhristu akhazikika lipangidwe musanayambe kukambirana monga malipiro a mbusa, katundu ndi malo omwe atangamangidwe ngati mopempherera.

- Khalani otsimikizika kuti kuchokera kuchiyambi kwa ntchito yatsopano kuti idzachulukitsidwa mwachangu, pogwiritsa ntchito njira iyi:-
 - ✓ Kuyamba ntchito zatsopano nthawi yomwe mukuphunzutsa anthu oyera mtima.

2. UTUMIKI WOPEMBEDZERA

Haward Synder ananene mu buku lake lochedwa “Guidelines for Urban Church Planting” kuti mpingo ukule ndi koyenera kukhala ndi mapemphero opatsa chimwemwe anthu. Palibe munthu amene amafuna kukhala pa mapemphero amukumbutse za maliri/chisoni. Chikhulupiriro chopanda chomwemwe ndi chisangalalo sichoona.

Mapemphero okhala ndi nyimbo zabwino amasangalatsa, izi sizikutanthauza kuti tisatsatire momwe mapemphero akuyenera kukhala. Kafukufuku wa dziko lonse yonwe ipanga mapemphero asangalatsa.

Nyimbo ndi mbali imodzi yakupembeza, timamupembeza mulingu ndife asati nyimbozo. Kupembeza kupembedza kumachitika mu mtima mwa munthu ndipo kumaunetsadwa m’njira zosiyana.

Mipingo ina imagwiritsa ntchito nyimbo ya chikhalidwe ndipo ina amagwiritsa ntito makolasi opembedzera.

Tikhulupira kuti tiyenera kulemekeza miyambo ya anthu komanso chikhulupiriro cha mpingo. Posatengera za mtundu wa nyimbo womwe mpingo wasankha, ndikoyenera kuti mapemphero akhale osangalatsa komanso amphamvu.

Mipingo ina ya mu Africa imagwiritsa ntchito zida ngakhalenso kuvina kutsogolo nyhawi ya mapemphero. Ndi kulakwitsa nunena kuti misamachite izi chifukwa choti simomwe timachitira ku United States, Brazil, India kapena kulikonse.

Ngati mbali iodzi ya kupembeza, mpingo uyenera kubatiza anthu komanso kukhala ndi mgonero wa ambuye. Dr Charles Brock, mu buku lake lochedwa “indigenous church planting” potengera zinthu zofunika ziwiri, iye anaonapo izi: Kuti ubatizidwe uyenera kukhala.

- a) Munthu woyenera – Akhale amene walapa machito ndi kuyika chikhulupiriro chake mwa khristu yesu ngati mbuye, mpulumutsi di mkalapakati wake. Baibulo mulibe ndime (vesi) imene imene imakhala kuti mwana ayenera

kubatizidwa limayankhula momveka bwino kuti ayenera kubatizidwa ndi iye amene watembenuka mtima. Mwana sangathe kumulandira yesu khristu za nkhani za momwe mungafalitsire uthenga wabwino ndikutsogolera maphunziro a baibulo

3. UTUMIKI WAKULALIKIRA

Mpingo umasowekera ulaliki wapadera kuti ukule. Mutha kugwiritsa ntchito dongosolo la mbukuli kapena ayi. Chofunikira kwambiri n di chakuti mpingo utenge mbali pokumana ndi anthu omwe akufuna kumvetsetsa za uthenga wabwino mdziko lonse osati kuwadikira tsiku la Mulungu lokha. Oyambitsa akusoweka kukhala ndi utumi oyendera anthu womwe umaphunzitsa a khristu kufikira otayika ndi kuwalalikira ndi cholinga chofuna kuwapulumutsira kwa Khristu m'malo ena osati ku tchalitchi kokha.

4. UTUMIKI WA KUTUMIKIRA

Ukhale Kuti ukule ndikoyenera kuti mpingo ukhale ndi dongosolo limene lingabweretse otembenuka atsopano pamodzi ndi kuphunzitsa atsogoleri m'modzim'modzi kapena ngati gulu. Oyambitsa aphunzitse atsogoleri kukhala mchikhulupiliro ndi kuwasula m'magawo atchito monga: mapemphero, kuchitira umboni, kupindula miyoyo kwa Khristu, kutsogolera maphunziro a baibulo am'makomo, kuphunzitsa anthu baibulo ndi zina. Chofunika ndi chakuti otumikira oyambitsawa nthawi zonse azitenga atsogoleri kapena otembenuka mtima atsopano pamene akupita kukagwira ntchito. Mwachitsanzo, okhulupilira atsopano apiti re limodzi ndi oyambitsa pamene iye akutsogolera maphunziro a baibulo m'makomo mwa anthu omwe sanamulandire Khristu kukhala Ambuye wawo. Mtsogoleri atsatiye oyambitsa ndi kuwona momwe akuperekera umboni, akutengera anthu ku chipulumutso kwa Khristu ndi zina.

Pali zinsinnsi ziwiri kuti utumiki ukhale wabwino. Choyamba, phunzitsani anthu paokhapaokha kapena m'magulu ang'onoang'ono. Chachiwiri ndi koyenera kuwatenga anthu pa mene mukufalitsa uthenga wabwino.

5. UTUMIKI WOSONKHANA PA MODZI

Kuti mpingo ukule, ndi koyenera kuti mpingo ukhale pamodzi pamene pali chikondi chenicheni pakati pa anthu ake. Pamene alendo afika mtchalitchi amve chikondi cha Mulungu ngakhalenso pakati a nthu a mumpingomo ngati pali zowawa, chidani ndi magawano ndi zosatheka kuti mpingo ukule. Mtendere ndi chikondi ndi zofunikira kwa alendo kuti awone umodzi wa mumpingo ndi kumva kulandilidwa.

6. UTSOGOLERI WOYERA

M’busa wina amene anali ndi mpingo wa anthu zikwi zinayi (4,000) wa ku United States anafunsidwa kuti, “Kodi pali kusiyana kotani m’busa kukhala ndi mpingo wa anthu makumi anayi (40) ndi wina amene ali ndi mpingo wa anthu zikwi zinayi (400)? ”

Yankho lake linali loti “Utsogoleri”

Ndichofunika apa kuti oyambitsa akhale ndi ganizo lophunzitsa anthu kuti agwire ntchito ya Mulungu osati kuchita zinthu payekha. M’busa angayendetse china chilichonse pa mpingo wa anthu 30 mpaka 80 imafika nthawi chifukwa chakukula kwa mpingo kumakhala kovuta kuyendetsa pokhapokha ataphunzitsa anthu ena njira za utsogoleri. Agawire maudindo anthu okhwima mu nzeru (luntha) ndi ophunzitsidwa bwino. Ntchito yaikulu ya ophunzitsa imakhalano ophunzitsa.

IX. ZIZINDIKIRO ZA MPINGO WA CHIPANGANO CHATSOPANO

Kukhazikika paokha panso pa utsogoleri wa Mulungu ichi ndi chinthu chabwino kwa omwe amakhulupilira ulamuliro wa anthu ambiri. Zotsatira za njirayi mu umoyo wa uzimu ndi zofunika pakakhala olephera mbali imeneyi chidwi chokhazikitsa mpingo watsopano, wokhazikika sichimatheka.

Kulephera kupereka udindo kwa otembenuka mtima zimalepheretsa kuyambitsa mpingo watsopano. Ndizosatheka kuti olalikira oyambitsa athe kuyesera kukhazikitsa mpingo watsopano ndikudzera mwa mzimu woyera kuti oyambitsa apatse maudindo olalikira, ophunzitsa, otsogolera kwa anthu a mu mpingomo. Pakuti mpingo wangoyamba, uyenera kuthandizidwa ndi oyambitsa. Mpingowu ndi umene uzipanga zisankho zawo m’ malo mwa gulu lotumikira ndi oyambitsa. Kodi izi nkutheka bwanji?. Izi ndi zotheka chifukwa oyambitsa amakhala akulangiza ndi kuphunzitsa mpingo wokhazikika kuchoka pachiyambi.

Ena atha kunena kuti mpingo sungathe ndipo sungathe kupanga zisankho pa iwo wokha. Posatengera kuti mpingo wa masabata atatu sungafane ndi mpingo watha zaka khumi (10) ndizothceka kupanga zisankho motsogozedwa ndi atsogoleri alutha mu mzimu. Ntchito ya oyambitsa ndikukhal opereka uphungu osati opanga zisankho. Aphunzitse ndi kulondoloza mpingo kuti usalakitse. Ngati mpingo ukulakwitsa, iye afunika kukhala ndi utsogoleri wamphamvu kuti

asalakwitse komabe, oyaambitsayo alole kuti mpingo upange zisankho pawokha.

ZINA ZOMWE TINGATSATE NDI IZI:

1. Otumikira oyambitsa alowe mu mzinda ndi kuitanira anthu kwa Khristu podula ulusi wake, kuvutika kumatha. Zotsatira zake gulugufe wake zamakhala wofooka ndipo sakhalitsa nthawi yayitali. Othandizayo amakhala kuti waswa lamulo, ngati munthuyu adakalola kuti gulugufeyu avutike, chirombochi chikadakhala champhamvu, chowoneka bwino ndi chokhwima bwino.

Pamene okhulupilira avutika, kuyenda mchikhulupiliro ndi kutsata Mulungu, ndi kumdalira Mulungu kuti awapatse zosowa zawo, adzakula mchikhulupiliro chawo ndipo adzakhala chimene Mulungu amafuna akhale. Mpingo yochuluka ili ndi chidzindikiro ndi dzina kutsogolo kwake. Mwachitsazo “First Baptist Church” zimamveka bwino akati “First Baptist Church imasonkhana pano.” Kodi pali kusiyana pazizindikirozi. Chidzindikiro coyambacho chikudziwitsa kuti nyumbayo ndi tchalitchi ndipo chachiwiricho chikudziwitsa kuti mpingo ndiye annthu ndipo atha kukumana m’maiko penapaliponse.

Tiwone fomu iyi yomwe ikusonyeza zomwe zinngataike kobzalaa mpingo umodzi

2. Adzaphunzitsa maphunzitso a baibulo ndi ziphunzitso zokhazikika pogwiritsa ntchito njira zosalunjika, nthano kapena njira zina.
3. Otembenuka mtima atsopano atumikiridwe ndi kubatizidwa.
4. Mzimu woyera udzutsa atsogoleri ngati angasiye iwo (Mzimu Woyera). Otembenuka mtima atsopano aphunzira ziphunzitso za baibulo.
5. Otembenuka amene agwirizana mchikhulupiliro adzapanga dongosolo la kuyamba mpingo.
6. Gululo limasankha mtsogoleri wake.

B. Kudzidalira paokkha pansi pa utsogoleri wa Mulungu tiyenera kuwaphunzitsa okhulupilira za chakhumi ndi chopereka . Werengani ndikulingalira Malaki 3 v 8 – 10 pamene mpingo ukuvutika komanso kumenya nkhondo umakula. Charles Brock, akulongosola Buku lake lotchedwa “Indegenous Church Planting” kuti zimakhala bwanji ngati munthu ayesera kuthandiza kutulutsa gulugufe mchisa chake. Gulugufe amavutika kuti achoke, m’ malo mwake ndipo munthu amayenera

kungoyang'ana. Ngati iye saupeza mtima ndi kuyesera kuthandiza chirombochi pogwiritsa ntchito njira zachikhalidwe.

Malipoti a anthu odzala mpingo _____ x 12 Months (Miyezi 12) x 7 years (zaka 7) =

Nyumba yomwe iwo akukhala pa mwezi _____ x 12 x 7 years

Katundu _____

Building (Nyumba) _____

Zonse pamodzi pa mpingo umodzi _____

C. Kupatsa motsongodzedwa ndi Mulungu

Mpingo wa chipano chatsopano ukhale wopereka. Pa chikhalidwe chake ugawane ndi ena. Mpingo wotere umakhala ukulalika ndipo umakhala ndi chidwi choyambitsa mipingo.

Ndimomwe dziko lasokonekera tiyenera kukhazikitsa mipingo yatsopano yomwe idzale inzazke kuti tikafikire anthu ochuluka m'mizinda.

Poyamba, Oyambitsa amakhala mlaliki. Amapu;lumutsa miyoyo, amitumikira ndi kuphunzitsa okhulupilira atsopano ziputsitso za chikhulupiliro. Kachiwiri, ndi kumupempha Mulungu kuti adzutse atsogoleri ndi kuwaphunzitsa kuti akayambe ntchito zatsopano m'malo oyandikira ndi m'mizinda. Mchitidwe upitilire kuphunzitsa atsogoleri ndi kupanga magulu osiyanasiyana kukhala mipingo. Ayenera kusiyira ntchito kwa atsogoleri koma kupitiliza kuwayendera ndi kuwalimbikitsa.

X. MATHERO

Oyambitsa kulalikira amene afuna kupambanira podzala mipingo achite izi:

- a) Akhwime mu uzimu, akonzekere ndikuphunzitsidwa bwino.
- b) Adziwe kukhazikitsa ndi kutumikira gulu lolalikira.
- c) Apulumutsire miyoyo kwa Khristu
- d) Ayambe mapemphero mosangalala ndi mokondwera.

- e) Adziwe kutsata ndi kutumikira okhulupilira atsopano
- f) Adziwe kuphunzitsa atsogoleri atsopano
- g) Adziwe kubatiza okhulupilira atsopano ndi kuchititsa mgonero wa Ambuye.
- h) Aphunzitse anthu wamba momwe angapulumsire anthu ndi kutsogolera maphunziro a baibulo ku nyumba za osakhulupilira.
- i) Aphunzitse atsogoleri kuti atsogolere mpingo watsopano.
- j) Phunzitsani mpingo kukhala, odzidalira, okhazikika ndi ogawana ndi anzawo
- k) Phunzitsani okhulupilirra momwe angapangire magulu olalikira kuti ayambe ntchito zatsopano.

MATHERO A GAWO LOYAMBA LA BUKULI

ZOFUNIKA KUZITSATA

MUNGAWAPHUNZITSE

BWANJI ANTHU

ZOFUNIKA KUZITSATA

MUNGAWAPHUNZITSE BWANJI ANTHU

Mbali ino yabukuli lifotokoza m'mene mlaliki oyamba wina angayendetsere mpingo. Njira zabwino zoyendetsera mpingo zimatsogoleredwa ndi mzimu oyera. Izi zimatheka chifukwa atumikiwo aatsogoleredwa ndi mzimu oyera m'mene zinalembedwera mu chipangano chatsopano. Atumiki oyambawa akugwiritsa ntchito njira zabwino zatsopano, izi:

- i. Tingayambe bwanji magulu atsopano
- ii. Tingayang'anire bwanji anthu ofuna za mtendere
- iii. Tingawasonyeze bwanji chikondi cha Mulungu pamaso
- iv. Tingalitsatire bxwanji buku loyera

A. Kuwaphunzitsa anthu osankhulupilira

Kusunga mbiri yabwino ya Yesu Khristu yofalitsidwa ndi Christy Brawner

B. Kutsata bwino lomwe ziphunzitso kwa okhulupilira atsopano

- i. Kuyamba moyo watsopano yolembedwa ndi Christy Brawner
- ii. Mlaliki oyamba ndi mzimu oyera
- iii. Mlaliki oyamba ndi pemphero
- iv. Mlaliki oyamba ndi chipulumutso
- v. Mlaliki oyamb a ndi umboni
- vi. Mlaliki oyamba ndi utumiki kudzera mu uthenga wabwino

TINGAYAMBITSE BWANJI MAGULU KAPENA MATCHALITCHI ATSOPANO?

Pamene mwakumana ndi gulu lanu koyamba ndi nthawi yomwe mungawaphunzitse njira zinayi zofunika.

MUNGAYAMBE BWANJI?

Atumeni kukafunafuna nkhosa zotaika zomwe zomwezikufuna chipulumutsokenako muyambe kuwaphunzitsa za chikondi ndi chisomo cha Mulungu. Kenako mudzikumana nawo mulungu ndu mulungukuwalalikira za Ambuye.

Pamene ntumiki walowa m'malo achilendo aziziwa kuti iye akutsogoleredwa ndi mzimu oyera kuti apeze anthu omwe ali ndi njala yofunafuna Ammbuye

Mulungu alipaliponse kulowa m'mitima ya anthu kuti akhale ndi chikhumbokhumbo chofuna mau a Mulungu.

Ntchito ya ntumiki ndiyomphweka tsopano chifukwa mzimu oyera walowa kale m'mitima ya anthu omwe ali ndi njala yofuna mawu a Mulungu.

Pali njira zambiri zomwe sizidzasintha, Uthenga wa buku loyera sumasintha njira zokhazo zolalikira uthenga ndi zimene zimasinthatintha

Njira za buku lino zimagwira ntchito motsogoleredwa ndi mzimu oyera. Zofunika kuyamba ndikukhala mipingo yozidalira pawokha motsogoleredwa ndi mzimu oyera monga:

- i. Ozitsogolera tokha motsogoleredwa ndi Mulungu
- ii. Ozidalira tokha motsogoleredwa ndi Mulungu
- iii. Ofufuzafufuza tokha motsogoleredwa ndi Mulungu

Ichi ndiye cholinga chathu. Kuti tifikire cholingachitiyenera kutsata njira za buku loyera zomwe zimafikira ku mitundu yonse.

TINGAWAPEZE BWANJI ANTHU OFUNA MTENDERE?

Mtumiki azikhala ndi chikhulupiliro kuti mzimu oyera amamutsogolera iye ndikulowa m'mitima ya anthu otayika

Mtumiki ayenera kusankha dera loti alifikire ndi anthu a m'malo osiyanasiyana monga m'misewu, mnyumba zogulitsira mowa, nyumba za anthu ndi pena paliponse.

Chiwerengeronso chikhoza kugwiritsidwa ntchito. Ndi ntchito ya Mulungu kutembenuza mitima ya anthu otaika.

Mtumiki pa iye yekha sangathe zimenezi, ndi mzimu oyera okha umene uli ndi mphamvu zotembenuza mitima ya anthu ndikuwaululira zinsinsi za Yesu Khristu.

Ndi udindo wa mpingo woyamba okhazikika kupeza anthu amene mitima ndiyosinthika ndi mzimu oyera.

Ndi udindo wanthu kukhala maso patsogolo kupeza anthu ofuna Mulungu ndi mtendere wa mu mtima.

Yesu adamutcha munthu otere munthu wantendere pa Luka 10: 5-6 mawu akuti mukalowa nyumba choyamba nenani kuti mtendere ukhale munyumba muno. Ngati munthu wantendere ali mnyumbamo mtenderenso udzakhala mwa iye. Ngati zitero mtendere udzabwelera.

Atsogoleri ayenera kumapita kumadera nkumakanena nkumakanena kuti ndilipano kutumikira mau a Mulungu, muli okozeka?

Ngati munthu ayankha kuti eya ndiye kuti munthu ameneyo ali ndi mtendere

Aloreni kuti asankhe malo oti mukakambirane mawu a Mulungu.

Chifukwa chiyani tikuchiita izi?

Ndondomeko iliyonse tiyambire pamene tikufuna kukhazikitsa mpingo kuti uddzakhale odzidalira okha. Mapemphero atha kuchitikira pansu pa mtengo, mnyumba mwa munthu kapenanso pabwalo. Choncho ndikofunikira kwambiri kukhala ndi malo amodzi okumanirana mulungu uliwonse.

Izi zimathandiza kuti anthu asamasokonezeke

Ndibwino kuti mtumiki asayambe msonkhano ndi anaokhaokha popanda akulu akulu.

Chiyambi cha mtumiki ntchito yake ikhale kutumikira makomo ndipo zidzathandiza kukumana ndi anthu osiyanasiyana komanso misinkhu yosiyanasiyana.

Cholinga choyambilira cha mtumiki chisakhale kuti iye aphunzitse koma kumagawana nawo mawu a buku loyera anthu amene akumana nawo.

Iye akhale mtsogoleri wa anthu amene akukumana nawo. Akatero ndiye adzafesa mbewu zokwanira

Mzimu woyera udzadzera mwa iye ndikutembenuza anthu mtima.

Imodzi mwa njira zopezera anthu amene ali othodwa ndi olema ndikuwafunsa mafunso a Mulungu.

Amene avomere, mtumiki apite kunyumba kwa anthuwo ndikuwatsogolera utumiki

Choyamba mtumiki akambirane ndiena kenako afunsane motere:

MAFUNSO AMUTHU YEMWE SANATEMBENUKE MTIMA

1. Ndingakufunsemi mafunso a zauzimu?
2. Mumaziwapo chiyani pa za Mulungu?
3. Mumafuna mutaziwa mulungu kwathunthu?
4. Ndingagawane nanu pa Mulungu ameneyu

MAFUNSO OKHUDZANA NDI KHRISITU

1. Ndingakufunsemi mafunso okhudzana ndi zauzimu?
2. Kodi munamulandira Yesu ndi kukhala mpulumutsi wanu kapena mudakali pa chisankho chotere.
3. Kodi mutamwalira usiku walero mukalowa kumwamba?
4. Muli okozeka kulandira mau a Mulungu Mnyumba mwanu?

Tiyeneranso kugwiritsa ntchito nyumba zoulutsira mawu, kugawa timabuku tamawu a Mulungu ndiponso misonkhano ikuluikulu ya mawu amulungu kuti tifalitse uthenga wabwinoponse

Izi ndi njira zina koma mtumiki oyamba ndi gulu lake amafunsa onse amene ali ndi chidwi ndi uthenga wabwino wa mawu a Mulungu kwa onse amene alandira mzimu oyera.

GAWO LACHIWIRI:

TINGAONETSE BWANJI CHIKONDI CHA MULUNGU KWA ANZANTHU?

Yohane 13:34-35

Buku la Yohane 13:34 Yesu akupereka lamulo latsopano kuti tiyenera kukondana wina ndi mzake. Ndipo akutilamula kuti ife tidzikondana wina ndi nzake m'mene Ambuye wanthu Yesu Khristu amatikondera.

Funso ndi ili: Yesu amatikonda motani?

Pali njira zambiri koma bukuli tikamba ziwiri zokha.

CHIKONDI CHOPANDA MALIRE

Mateu 9:9-13

Yesu anamuuza Mateyu kuti amutsate, iye Mateyu anali olowelera koma chifukwa choti Yesu amakonda ochimwa, amamukonda mateyu.

Yesu anaona munthu ovulala, olowelera komanso otaika mu umzimu mchifukwa chake Yesu anamuuza mateyu kuti amutsate iye. Iwo adapilira ndi chikondi chawo.

Yesu adaonakuti adamukonda kwathunthu kotero kuti atha kulora kufa naye limodzi.

Yesu atikonda tonse posayang'anira kuti ndife ndani komanso kuti timachita zotani.

Yesu amatikonda chomodzimodzi kwa omutsatira ngakhale amene samutsatira iye. Iye amakonda aliyense

ADALORA KUTAYA MOYO WAKE

Mateyu 14:13-14

Ngakhale kuti nthawi zambiri Yesu amakonda kukhala yekha iye ndiokonzeka kuthandiza onse amene akufuna kutsata iye. Kwa omupempha iye amapatsa zomwe anthu afuna. Iye ndiodzipereka kwathunthu othodwa, olumala komanso otaika. Iye ndiokozeka nthawi zonse kuthandiza aliyense.

Nafenso tiyenera kumakondana wina ndi nzake chimodzimodzi

CHIKONDI CHOPANDA MALIRE

Mu buku la Levitiko 19:18

Mulungu atanena za Lamulo loti konda nzako m'mene umadzikondera iwe mwini.

Buku la Luka 10: 29

Ophunzira adafunsa Yesu kuti m'nansi wako ndani?

Yesu anamuphera fanizo kuti panali munthu wina amene anamenyedwa ndi achifwamba ndipo munthu wina anadutsa mosasamala ndipo munthu wina anadutsa nayima nasamala ndi kupita naye kwa munthu woti amusamale ndipo iye

adzalipira zomwe zidzafunikire. Apo Yesu anfunsa kuti kodi munthu uja m'nansi wake anali ndani?

Monga inu ophunzira a Yesu mulibe m'dani kondani aliyense monga mudzikondera inu eni. Kaya m'nansi kaya m'dani , olemera kaya osauka , owoneka bwino kaya waumve

Mulungu ndiye chikondi Anaonetsa chikondi chake chonse pa mtanda.

Mulungu akufunitsitsa kuonetsa chikondi chake chonse ku dziko lapansi. Akuonetsa chikondi chake motani lero?

Iye akufuna kuonetsa chikondi chake chake kudzera kwa omutsatira monga inuyo. Nanga inu mukuchitapo chiyani pa zachikondi?

Mungathe kuwafikira othodwa ndi otaika pofuna kusonyeza chikondi cha Mulungu mwa njira yooneka ndi maso?

Yohane 13:35. Pakuti anthu adzadziwa kuti ndinu ophunzira anga ngati mukondana wina ndi nzake.

Ngati musonyeze kukondana kwanthunthu anthu adzaona chikondi mwa ife ndipo adzatha kusiyanitsa kwathunthu.

Anthu adzatsekula mitima yawo ndipo tidzabweza nkhoa zosochera, pomva ndikulandira choonadi. Chikondi chidzathandiza kutsekula mitima yathu kuti tigawane uthenga wabwino ndi adzathu. Choncho tigaonetse bwanji chikondi kwa anzathu? Tingawatumikire bwanji adzathu? Tingawatumikire bwanji za chikondi cha Mulungu anthu omwe timacheza nawo. Nganizirani m'mene mugadabwitsire anzanu pa za chikondi cha Mulungu. Dziko likufuna muchitepo kanthu pofuna kusonyeza kuthokoza kwanu pazachikondi cha Mulungu. Koma ngati tikuntumikira iye ndiye kuti tikusonyeze kuthokoza kwathu.

Tiyeni tipite ndikunena za chikondi cha Mulungu kwa amene atsekula mitima yawo ndikufuna za uthenga wa Ambuye Mulungu adzakuwunikirani za anthu amene akufuna za mtendere.

TINGATSATIRE BWANJI ZAPAKHOMO

Palifundo zina zofuna kuzitsatira pamene tikutumikira makono.

Machitidwe 16:31 akuti khulupilirani Ambuye Yesu Khristu ndipo mudzapulumuka.

Oikos ikutanthauza tikupempherera pakhomo kapena pa bwalo. Munthu wina aliyense amakhala pakhomo.

Pamene mwapeza munthu amene akufuna za mtendere, mudziwe pakhomo pake komanso banja lake lonse.

Mwachitsanzo, ngati munthu wa Mulungu ali ndi anthu khumi panyumba pake onsewo muwadziwe bwino.

TINGAWATSOGOLELE BWANJI ANTHU ZA BUKU LOPATULIKA ANTHU OSAKHULUPILIRA

KUKAMBIRANA ZA UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU

Pamene mwapeza munthu amene ali ndi chilakolako komanso njala yofuna mawu a Mulungu mumukozere nthawi yomamuyendera pakhomo pake nthawi ndi nthawi, mumulimbikitse kuti iye ndi m'banja lake adzikhala nawo pamapemphero omwe adzikhhalapo.

Adziwitseni kuti kukumana kwawo kukhala kwa masabata asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu. Sikofunikira kukambirana mochepea.

Pali njiranso imene ingatsatidwe pogawana mawu a Mulungu. Njirayu ndikukambirana za uthenga wabwino. Njirayi ndiyabwino kwa anthu ame ndi osiyana kwane samawerenga. Zokambirana zake zikhale nkhani zabwino zopatsa chikoka kwa munthu omvera. Dziwani kuti anthu mukukambirana nawo ndi oti sanadziwe Yesu ndipo ndi osiyana kwathunthu ndi amene anamudziwa kale Yesu. Choncho anthu amenewa ndikofunika kuwabweretsa chifupi ndi Mulungu mwapang'onopang'ono.

Tiyambe kuwauza kuti buku loyera ndi nkhekwe ya mawu a otilenga. Bukuli linalembedwa ndi aneneri osiyanasiyana. Buku limeneri limatiuza za chikondi cha Mulungu komanso iye ndindani popeza iye analipo, alipo ndipo adzakhalapo. Iye ndiye choona

Chachiwiri auzeni okonedwa kuti buku loyera ili ndi mbali ziwiri chipangano chatsopano ndi chakale. Auzidwe kuti mu chipangano chatsopano muli zotani komanso mu chipangano chakale mulizotani.

Chachitatu tiyeni tiwasonyeze m'mene angagwiritsire ntchito buku loyera. Tiwasonyeze m'mene angapezere masamba a bukuli.

Koyamba apeze buku la Mateyu ndipo tiwasonyeze ndime za bukuli. Tiyeni titsatire zinthu izi.

1. Tiyeni pamene tikugawana nawo anzathuwa za mawu a Mulungu tigawane nawo mwachikondi ndi mwaulemu.
2. Tiyeni tiyankhule nawo modekha koma asalalikire kwa munthu m'modzi.
3. Pokambirana tisamakangane kapena kutsutsana koma lorani mzimu oyeru ugwire ntchito yake yomenya nkondo yotsekula mitima ya anthu.
4. Tisaweruze munthu kapena kuzitenga ife olungama pakuweluza ndiye mwini wake Mulungu.
5. Kukumana kuli konse kudziyamba ndi pemphero lopempha Mulungu kuti pakhale kumvetsetsana pazokambirana zimene zilipo.
6. Nthawi zonse tidziyamba ndi chiganizo chochokera kabuki ndipo anthu akambirane pa zachiganizo chomwe chawerengedwa
7. Mtsogoleri afunse mafunso pazimene akambirana kuti awone ngati anthu amvetsa.
8. Awernge za choonadi ndipo anthu apatsidwe mpata okambirana komanso kufunsa mafunso pazimene sakumvetsa. Ndipo khalani osamala posakangana komanso osatsutsana pa zokambirana.
9. Mukatha kukambirana za choonadi khalani ndi nthawi yogawana pazimene mwawerenga.
10. Aliyense apemphe zosowa zake funsani gulu lanu m'mene likutukukira ndipo aliyense amulore Yesu kuti akhale mpulumutsi wake
11. Pomaliza phunziro lomalizila la chisanu ndi chiwiri aliyense akhale ndi mwawi omulandira Yesu kwathunthu.

KALONDOLONDO KWA OKHULUPILIRA ATSOPANO KUYAMBA MOYO WATSOPANO NDI YESU KHRISTU

Mateyu 28:19 ndi Timoteo wachiwiri2:2

Yesu akutilamula kuti pitani mukalarikire osati kungowasintha chabe.

Panthawi yothandizana za mawu a Mulungu anthu auzidwe kuti ndikofunika kupereka miyoyo yathu kwathunthu kwa Mulungu. Utumiki uyenera kuyamba pompopompo kuti ukhazikike. Tikatero ndiye kuti tidzakhala moyo wochuluka ndipo wantendere

Chinthu choyamba tiyenera kuwalalikira kuti adziwe m'mene angagawire nthawi pa za Ambuye. Chachiwiri aphunzitsidwe za pemphero.

MFUNDO YOFUNIKA KWAMBIRI

Alaliki oyamba ali ndi mfundo zofunikira kwambiri. Panopa afika pomayamba msonkhano ndi onse amene adamaliza komanso osamaliza za mawu a buku loyera. Aliyense amene wangobadwa mwatsopano ayenera kukhala ndi nthumwi yake.

Nthumwi ya munthu aliyense ikhale ya chidwi kuti munthu akumuyang'anirayo akule mu uzimu ndipo zidzathandiza kuti mpingo ukule. Aliyense oyang'anira nzake akhale chida chenicheni ndipo akhale wachikhumbokhumbo chofunitsitsa kuyamba moyo watsopano

Chinthu chofunikira kwambiri ndikufufuza anthu ofuna za mtendere nthawi zonse ndipo ofuna kumamva mawu a Mulungu nthawi zonse.

SABATA LA ACHITATU

Mulungu umenewu ndi ofunika kwambiri.

Mtumiki wa Mulungu apereke mwayi kwa gulu lake kusankha okha owatsogolera sabata lotsatira.

Mtumiki wa Mulungu akhale nhandizi chabe owaunikira za utumiki mothandizidwa ndi mzimu oyera.

Gululo likasankha munthu owatsogolera , mtumiki amuphunzitse za m'mene zimakhallira ndipo adzikumana ndi gulu lake sabata lililonse.

SABATA LA CHINAYI NDI CHISANU

Mtsogoleri osankhidwa ndi gulu atsogolere gulu lake ndipo mtumiki asalowelerepo. Iye akhale ongomvera.

SABATA LA CHISANU NDI CHIMODZI

Mtumiki afufuze chifukwa chomwe sangamakhale nawo misonkhano ina ndi ina ndipo awauze anthu kuti msonkhanoo ukhalepo ngakhale iye palibe

KUSUNGA MWAMBO

Gulu lija likacheze ndi anzawo moongoleledwa ndi mtsogoleri wawo.

Mtumiki ayenera kukumana ndi gulu lake kuti amve m'mene amayendera kwa anzawo.

Mtsogoleri aphunzitsidwe mozama za utumiki ndipo azikawayendera anzake pafupipafupi. Izi zidzamuthandiza kuzama ndi kukhala chifupi ndi Mulungu.

MTUMIKI WA MULUNGU NDI MZIMU OYERA

Mtumiki Paulo amadalira mzimu oyera kudzela mwa mzimu oyera Paulo oyera adali ndi mphamvu zolalikira unthenga wachipulumutso ndipo amtha kuchita zozwizwitsa.

Paulo oyera mothandizidwa ndi mzimu oyera amatha kuyambitsa mipingo.

Nthawi zonse Paul Oyera amadalira mzimu oyera pochita zinthu.

POLOWA M'MIZINDA NDIKUKAMBIRANA NDI ANTHU ACHIDWI PA ZA UZIMU.

Mzimu oyera amatsegula zitseko kudzera mu njira zosiyanasiyana anthu osiyanasiyana ndi zochitikanso zosiyanasiyana kuti athe kulumikizana ndi Mulungu . Muzinda uliwonse umakhala ndi anthu achidwi ndi unthenga wabwino wa Mulunguakugwira ntchito paliponse ndipo mzimu oyera akumatsegula mitima ya anthu yosochera. Mzimu oyera umapukuta ndi kuyeretsa machismo athu ndikubadwanso mwatsopano mwa Yesu Khristu. Mzimu oyera ndi amene amatilumikizitsa ndi Mulungu. Pamisonkhano ya atumiki a Mulungu mtumiki akhale ndi mwayi ofufuza atsogoleri ena ndi kuwaphunzitsa. Ntumwi Paulo akalowa mu mzinda amatha kukhala masabata awiri kapena atatu kutsitsimula mizimu ndikupeza atsogoleri atsopano otumikira magulu atsopano.

Mtumiki ayenera kudalira mzimu oyera pofuna kupeza atsogoleri.

GULU LATSOPANO

Mpingo umadalira mzimu oyera. Ichi ndi chiyambi. Ngati mpingo ndi chida chodalira mzimu oyera utha kupeza anthu ambiri ndi mphatso zosiyanasiyana zomwe zili zofunika mumpingo.

Mphatsozi zikupezeka mu Akorinto 1:12, Aroma 12:6-12 komanso Petulo oyamba

POTULUKA MU MZINDA

Mtumiki ayenera kudalira mzimu oyera pamene akutuluka mu mzinda. Pamene mtumwi Paulo amatulika mzinda amtha kusiya ntchito ya Mulungu m’manja mwa atsogoleri enna chifukwa amaziwa kuti choona chake asiya ntchitoyo m’manja mwa mzimu oyera. Kuti tigwire bwino ntchito ya Mulungu, mtumiki ayenera kuima nji ndipo adzazidwe ndi mzimu oyera.

Werengani Aefeso 5:18 mawu akuti “musedzere naye vinyo m’mene muli chitaiko komatu mudzale naye mzimu.”

1. NTCHITO ZA MZIMU WOYERA

Mzimu suoneka ndi maso: Aheberi 9: 14

Mzimu oyera aliponseponse: Masalimo 139:7-10

Mzimu oyera uli ndi mphamvu zonse: Luka 1:35

Mzimu oyera ndi wokhulupilika: Yohane 14:12,26

Umu ndi m’mene Mulungu amagwirira ntchito.

2. NTCHITO ZA MZIMU OYERA KWA ANTHU OTAIKA

Mzimu oyera akunenetsa kuti Yesu ndiye choonadi Yohane 15:26-27.

Mzimu oyera adzatsutsa dziko lapansi za machismo ndi zachilungamo ndi za chiweruziro.

3. NTCHITO ZA MZIMU OYERA KWA AKHRISTU

Mzimu oyera umapereka chikhulupiliro za moyo osatha. 1 Akorinto 1:22
Aefeso 1:13-14

Mzimu oyera umapulumsa akhristu Tito 3:53

Mzimu oyera umamasula ku lamulo la uchimo ndi la imfa. Aroma 8:2

Mzimu oyera umalimbikitsa akhristu Aefeso 3:16

Mzimu oyera umalimbikitsa ndikumasula kwa akhristu Machitidwe 8

4. KUDZADZIDWA NDI MPHATSO ZA MZIMU OYERA.

Akhristu onse ayenera kukhala ndi mzimu oyera: Aefeso 5:18

Chipatso chamzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima ndi chikhulupiliro.

Ntchito za mzimu oyera ndi kugawa mau a Mulungu ndi kutilimbikitsa: Machitidwe 4:29,31

ZIMENE MZIMU WOYERA AFUNA

Mzimu woyera umafuna kuti munthu apulumuke: Machitidwe 2:38

Mzimu oyerera umafuna kuti munthu alape machismo ake onse 1 Yohane 1:9 ,
Masalimo 66: 18

Mwachikhulupiliro munthu apemphe mzimu woyera kuti ukhale ndi kulamulira
Iye. 1 Yohane 5:14-15, Aroma 1:17

Munthu azimvera Mulungu nthawi zonse masiku amoyo wake onse :
Machitidwe 5:32

Buku la malembo oyerera limatsimikizira ndikunenetsa kuti munthu ayenera
kukhala ndikutsogoleledwa ndi mzimu oyerera monga m'mene Davite amachitira.

Samueli 16:13 Mphamvu za mzimu woyera zimachokera kwa Mulungu.

Monga Mulungu akutilimbikitsira lero Davitenso anadzazidwa ndi mzimu
oyera wa Mulungu chifukwa Mulungu anali naye cholinga.

Mulungu ali ndi cholinga pa munthu wina aliyense.

Mphamvu za mzimu oyerera sizimachokera ku ndalama, maphunziro, kutchuka
kapena udindo wa munthu (Washington DC) koma kwa Mulungu yekha.

1Samueli 17:45 -Kudalira mulungu nkokwanira ndipo sitisowa kudaliranso zinthu zina

Goliati anali okozeka kukagonjetsa pa nkondo. Iye anali wa mphamvu,
wodziwa nkondo anali ndi dzida komanso onenepa.

Davite sanali wa mphamvu, analibe zida, sanali onenepa analibe luntha la
nkondo ndipo sanamenyepo nkondo koma iye anati ndabwera kudzamenya
nkondo mudzina la Yesu Khristu wamoyo. Mulungu amene ali ndi asilikali
ambiri ku Israyeli.

Davite amalimba mtima chifukwa cha mzimu woyera ndipo izi ndizimene
zikufunika kwa ife.

Mulungu akatiitana kuti tigwire ntchito yake tiyeni tiyankhe mwachangu
chifukwa iye alinafe cholinga.

Mzimu oyerera ndi okwanira ndipo ndi chida chomwechingatithandize pogwira
ntchito yake. Izi ndiye zofunikira kwa ife.

1 Samueli 17:50- Mulungu alinako kuthekera mwa ife

Pakati pa Davite ndi Goliati adapambana ndani? Sizontheke kuti Davite mkupambana ayi anapambana ndi Mulungu. Mulungu alinako kuthekera mwa ife kuchita china chilichonse kudzera mwa ife.

1Samueli 17: 46- Mulungu amapanga zosatheka kukhala zotheka

Mulungu amapanga zinthu zosatheka kukhala zotheka kufuna kusonyeza mphamvu zake.

Mulungu ali ndi mphamvu mchifukwa chake adapangitsa Davite kugonjetsa Goliati kufuna kusonyeza kuti iye ndiyedi Mulungu wa Israeli.

Tikamulora Mulungu kukhala Mulungu mwa ife tidzakhala opambana nthawi zonse

MATHERO

Mutawerenga nkhani ya Davite ndi Goliati khalani ndi nthawi yokwanira kuwerenga ndime izi:

Okhulupilira ali ndi mzimu oyera kusonyeza kudzozedwa kwawo.

1 Yohane 2:20,27

2 Akorinto 1:22

Aefeso 1:13

Anatisindikiza chidzindikiro, natipatsa chikole cha mzimu m'mitima yathu

2 Akorinto 1:22

Aefeso 1:14

Pakutinso mwa mzimu m'modzi ife tonse tinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi

1 Akorinto 12:13b

Yohane 4:14,7:37-39b

Iye wakumwako madzi amene ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse. Koma madzi amene ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye Kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha.

Tiyenera kumvera amene anati, mukani kudziko lapansi lalikirani uthenga wabwino kwa olengedwa onse. Marko 16:15

Patulani iwo muchoonadi popeza mawu anu ndi choonadi. Yohane 17:17

Tiyeni tigwire ntchito mwachikhulupiliro popeza pokhulupilira pamenepo, iye amene anayamba adzaitiriza kufikira tsiku la Yesu Khristu.

Sulikusowa mu chaufulu chilichonse pakudikira vumbulutso la Ambuye wathu Yesu Khristu. 1 Akorinto 1:7

Pali mphatso zosiyana koma mzimu yemweyo ndipo pali mawutumiki osiyana koma Ambuye yemewyo. Pali chachitidwe osiyana koma Mulungu yemweyo.

Wochita zinthu zonse mwa onse. 1 Akorinto 12:4-6 Tiyenera kumvera Mulungu mu zonse potsatira mawu ake koma chipatso cha mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiliro, chifatso, chiletso pokana zimenezi palibe lamulo

ZOLINGA ZATSOPANO

Izi zimatipatsa njira za m'mene angakuzire mpingo.

Njira zabxwino ndi m'mene Paulo amachitira, ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezo uziike mwa anthu okhulupilira amene adzadziwa kuphunzitsa enanso.

ZOYENERA KUZICHITA

Izi zimatithandidza kuti tidziwe njira zoyenera kuzitsata pamene tikuchita chinthu maka magulu awiri.

Mu utumiki zimatithandiza kuona kuti tingayambe ndi kukuza uthenga motani kapena pamene tikupeza malo atsopano.

Izi zimachitika motere:

- Kupeza anthu amene akufunitsitsa chifundo cha Mulungu
- Kupeza ndi kugawana ndi amene akufuna mzimu oyera kuti ugwire ntchito mwa iwo.
- Kugawana uthenga wabwino kudzera mu maphunziro a buku loyera
- Kupereka makhalidwe abwino kwa okhulupilira kudzera mu buku loyera.

MAKHALIDWE

Tingapereke bwanji makhalidwe abwino kwa anthu a Mulungu kudzera buku loyera

ZOYENERA KUZITSATIRA:

Izi zimapereka chilimbikitso pa za uzimu kwa otumikira komanso kwa onse odzipereka kukuza tchalitchi.

Buku lopatulika ndi buku loyera momwe Mulungu amatiphunzitsa zachilungamo ndi m'mene tingakhalire ndi utumiki.

Tiyeni tiphunzitse zimenezi kuti zikhale chinthu chokhazikika komanso anthu amvetse kuti uyenera kuwatumikira ndi ndani mu utumiki wa Yesu. Tiyenera kupereka chitsanzo chabwino kuti cholinga cha mpingo anthu achidziwe.

Koma ndagwira ntchito panthawi imeneyo komanso adagwira ntchito ku dziko lonse la Brazil mu chaka cha 1989. Iye adapereka moyo wake onse pa mpingowu.

Sherry adapezeka ndi matenda okhuzana ndi minyewa ya mapapo, matumbo komanso mbali zina zofunikira.

Izi zidatulukidwa mwezi wa Seputembala m'chaka cha 1992. Iye atafunsidwa ngati akufuna kubwereranso kwa makolo ake ku America ndikulekana ndi Brazil mu moyo wake onse iye adati cholinga cha moyo wake ndi kumkwezeka ndikulambira Ambuye mu moyo wake komanso pa imfa Mulungu adandiitana ku Brazil ndipo ndikhala kumeneko.

Pa 4 Disembala mm'chaka cha 1993 Sherry adakomoka mwadzidzidzi ndipo adamwalira kumudzi kwawo ku Belo Horizonte mu zinda otchedwa Minas Gerais ku Brazil.

Sherry ndi munthu m'modzi amene adakhala ndi kumwalira mu choonadi cha Mulungu.

Koma iwo a Khilisitu, Yesu adapachika thupi ndi zokhumba zache ndi zilakolako zache. Ngati tili ndi moyo ndi mzimu, ndi mzimunso tiyende. Tisankhale odzikuza, outsana ndi akuchitirana kaduka.

ZOTI TIDZICHITA

- Tidzipemphera mwakachetechete
- Tidzipempha mzimu oyera kuti atilamulire zinsinsi ndi machismo athu pa moyo wathu.
- Tilape machismo onse omwe mzimu woyera watiululira.
- Tidzipereke kwatunthu kwa Mulungu ndi kumumvera iye.

UTUMIKI OYAMBA NDI PEMPHERO

Ndikovuta kukhala okhulupirika pamaso pa mulungu ngai sulimu pemphero. Mtumiki oyamba ayenera kumakhala nthawi zones ndi mulungu ngati chinthu choyamba pa moyo wake. Ngati satero ndikovuta kudziwa mulugu kwathunthu. Mtumiki ameneyu sadzayenda mchiyero, mochoona komanso sangalandire mphatso za mzim,u woyera.

Chonde satirani ndondomeko za mapemphero.

1. PEMPHERO NDI PEMBEDZERO

Buku loyera likunenetsa kuti mulungu ndiye wamkulu ndipo ayenera kulemekezedwa .

Masalio 48:1. Ndidzalemekeza mulungu nthawi zones.

Kumulemekeza kwake kudzakhala mkamwa mwanga kosalekeza.. moyo wanga uzatamanda miulungu. Ofatsa adzakummva nadzakondwera. Bukitsani pamodzi ndine ukuru wa mulungu ndipo tikweze dzina lake pamodzi. Masalimo 34:1-3. Timamutamanda mulungulamulungu liri lonse, koma machitidwe athu ndi otani kuchokera lolemba kufikira ku Loweluka? Buku loyera likuta koma inu ndi woyera, wakukhala m'malemekezo a Israyeli.

Kupembeza mkutani? kumpembeza ndi kumukwezaka mulungu monga iye oyenera kulandira ulemu wake.

Chithokozo ndi kuthokozamulungu pa zabwino zones amatichitira.

Kupemneza ndi chikhalidwe ndi machitidwe othokoza mulungu.

Buku loyera likuti wampembedza mulungu ayenera akhale odziletsa, wodziwala koma wachifundo. Sipolakwika kudziwala pamene tikutamanda mulungu. Ndipo mulungu wantendere yekha ayeretse inu konse konse, ndipo mzuu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zitsungidwe za mphuphu zopanda chilema pakudza kwacha kwa ambuy wathu yesu khristu. 1 Atesalonika 5:23

Pali kusiyana pakati pa kudziletsa ndi kupsa mtima. Kupsa mtima ndi kuonetsa mkwiyo pa wina zimene zimachititsa mpingo usokonekera. Buku loyera silikuletsa kupsa mtima koma kukhala kudziletsa.

A.NJIRA ZOTAMANDIRA MULUNGU

Kuimba nyimbo pogwiritsa mabuku woyera

Anthu ali ndi ufulu kuimba nyimbo pogwiritsa mabuku kapena kungoimba kuchokera mmutu monga ngati Oyera , Oyera.

Werengani ndime zisanu kenako siyani lingalirani kenako pezani matanthauzo a mawu ali mu nyimbo. Kerengani kachiwiri ndikuchita chimodzimodzi

B. KUIMBA NDI KUWERENGA NYIMBO ZOTAMANDIRA

Buku loyera likuti kudzilankulira nokha ndi nyimbo zauzimu kuyimbira ndi kuyimba molimba . ambuye muntima mwanu ndi kuyamika mulungu Atate masiku onse chifukwa cha zonsem'dzina la ambuye watyhu yesu khristu.

C.WERENGANI NDIME ZAMAPEMPHERO MU BAIBULO NDIKULINGALIRA PA MAWU.

Mulungu ambuye wathu dzina lanu liposadi padziko lonse lapansi. Inu ndinu amene munaika ulemelero wanu pa thambo la kumwammba. Ndime imeneyi ikutanthauza mulungu, mulungu dzina lanu lilemekezeke nthawi zones pa dziko lonse lapansi.

Ndime zina zam'buku loyera zimati mulungu ambuye wathu dzina lanu lliposadi nanga pa dzina lonsa lapansi..

2. KULAPA

Tisataye nthawi poganizira za machismo omwe tachita popeza mzimu woyera ndi amene amatikumbutsa zones zimene tamuchitira mulungu. Choncho chofunika ndikupempha mzimu woyera kuti utikumbutse ndipo tilape machismo onse popeza tikatro ndipamene tingayanjanenso ndi mulungu. Adzakhululuka machismo onse ndikuyeretsa ngati matalala. Pamene tikulapa achimo athu kwa mulungu mzimu oyera uzatikumbutsa ndikutichenjeza za kuopsa kwa machismo. Ife monga oyambitsa mpingo udindo wathu ndikuwasonyeza anthu za kusiyana kwa chikhulupiro cholimba ndi chikhulupiro chopulumutsa.

CHIYAMIKO

Buku loyera likuta musadere nkhwana konse, komatu muzonse ndipemphero ndi pembezero pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Afilip 4:6

KUMVA MAWU AMULUNGU

Moyo wanga, ukhale chete Mulungu yekha, pakuti chiyembekezo change chifumira kwa iye. Masalimo 62:5

Khalani chete ndipo dziwani kuti ine ndine Mulungu ndidzabuka mwa amitundu ndipo ndidzabukanso padziko lapansi.

Tingamve bwanji mawu a Mulungu amaperka matanthauzo awiri kwa okhulupilira tsiku ndi tsiku. Mawuwa amafika kudzera kwa mzimu woyera komanso Mulungu mwini wake. Choncho chikhulupiliro chadza ndi mbbiri za mwa mawu a Mulungu.

Ndichikhumbo cha Mulungu kufuna kumayankhula kwa wina aliyense wa ife tsiku ndi tsiku kudzera m'mawu ake komanso kudzera mzimu oyera.

Zina mwa njira zoyankhulana ndi Mulungu.

- A. Kuyamba kuwerenga mawu a buku loyera monga Aefeso
- B. Funsani Mulungu kuti akuonetseni choonadi mu ndime imene mwawerenga, Paulo ntumwi wa Khristu Yesu wachifuniro cha Mulungu kwa oyera mtima amene ali mu Efeso ndi kwa iwo okhulupilika mwa Khristu Yesu.

ZINA ZOSONYEZA CHIKHULUPILIRO

- 1. Paulo ndi okhulupilika mwa Yesu Khristu
- 2. Iye ndi mtumiki osakhidwa ndi Mulungu
- 3. Mawu oti Woyera amakhuzana ndi a Isirayeli
- 4. Akhristu amenewa anali okhulupilika kwa Yesu Khristu.

Mulungu akuyankhula kwa aliyense payekhapayekha kudzera mu zikhulupiliro zimenezi

- 1. Thomas Wade ndiwe mtumiki wa Yesu Khristu kuchokera pansu pa mtima wanga
- 2. Thomas Wade ndidakusankha mwakufuna kwanga
- 3. Thomas Wade, ndiwe woyera kumene umakhala ku Belo Horizonte, Brazil

4. Thomas Wade, ndikufuna kuti ukhale okhulupilika kwa Yesu Khristu.

TIPEMPHERE MAWU AMULUNGU MOBWEREZABWEREZA

Tinene pemphero ngati monga lochokera kwa Aefeso ponena kuti :

Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wanthu Yesu Khristu amene anatalitsa ife ndi dalitso lonse la mzimu m'zakumwamba mwa Khristu monga anatisankha ife mwa iye lisanakhazikike dziko lapansi, tikhale ife oyera mtima ndipo opanda chilema pamanso pake m'chikondi.

Mudzina la Yesu Khristu tapemphera, Amen.

Tikantha pemphelori kudzera mu njira zonse tithe kupitiliza ndi magawo ena amapemphero.

KUPEMPHERERA ANTHU ENA

Tiyeni tipemphe mapemphero athu kuchokera pa mtima.

Mwapemphero lonse ndipembezero mupemphere nthawi yonse mwa mzimu ndipo pochezera pamenepo tichezere oyera mtima onse.

Pembezero ndi pemphero lopemphelera anthu ena.

Nthawi zambiri pamene muli ndi mapemphero

Malemba akunenetsa kuti ngati m'dyerekezi amakhulupilira kuti Yesu ndi patali. Mawu oti **chikhulupiliro kapena kukhulupilira mu chigiliki ndiye kuti munthu wadzipereka moyo wake onse kwa Yesu Khristu kuti iye akhale mwa iye khilisitu.** Amene sachita zimenezi alibe chikhulupiliro.

Pepala loyamba: lilembedwe tsiku ndi tsiku ndipo kuseri kwake kwa pepalalo kulembedwe ana, makolo, achimwene ndi ena omwe ali oyandikira.

Tsamba la pepala lina lilembedwe :**Lamulungu** -ndipo kuseli kwake kulembedwe dzina la m'busa ndi mkazi , mphunzitsi wa ana kapena amene ali mkalasi mwanu ndikumawapempherera.

Pepala lachitatu lembani : **Lolembe-** ndipo ili lilembedwe maina a ana athu ndi anzathu.

Tsamba la pepalla lina lilembedwe : **Lachiwiri-** ndipo tilembepo maina a ananthu ena ali onse ndipo tiwapempherere.

Tsamba la pepala lina tilembep: **Lachitatu** – ndipo tilembepo maina a mipingo ndi atsogoleri a mipingo osiyanasiyana.

Tsamba la pepala lina tilembe : **Lachinayi**-ndipo tilembepo maina a atsogoleri a ziko.

1 Timoteo 2:1 ndi 2 Ndidandaulira tsono, poyambayamba achitike papembedzo, mapemphero, mapembezero, mayamiko chifukwa cha anthu onse, chifukwa cha maufumu ndi onse akuchita ulamuliro kuti m'moyo mwanthu tikhale n dikamtima ndi achetem'kulemekeza Mulungu ndiulemekeza monse.

Tsamba la pepala lina tilembe: **Lachisanu**- ndipo tilembe maina a anthu amene anagwa mu mpingo, kapena nkhoa zotaika ndipo tiwapemphere.

Tsamba la pepala lina tilembe: **Lowerika**-ndipo apa tilembe maian a anthu omwe timapemphera nawo ndipo tipemphererane.

Ngati mtumiki adzichita izi: ndiye kuti adzipemphera nthawi ndi tsiku lilonse pa Mulungu

Ena amkhulupilira kuti Aroma 16 ndi pemphero la Paulo kupempherera akhristu aku Aroma.

CHIFANIZIRO NDI MAWU A MULUNGU

Buku la Josha likunena kuti buku ili ndi la chilamulo lisachoke pakamwa pako koma ulingiliremo usana ndi usiku kuti usamalire kuchita monga mwa zonse zolembedwamo popeza ukatero udzakometsa njira yako nudzakometsa mwa nzeru. Josha 1:8

Kufunafuna ndikufanana ndi Mulungu ndikofunika kwambiri. Izi zimathandiza kukhala mchiyero nthawi zonse. Pamene tikhala m'chiyero tidzakhala opambana pa zonse. Kutu tikhale ndi Mulungu nthawi zonse tiyenera;

- A. Tizisankha lemba loti tiwerenge pa mulungu.
- B. Tidziwerenga buku loyera tsiku ndi tsiku
- C. Tipemphe Mulungu kutitumizira mzimu oyera kuti atiunikire pa limbo lomwe tikuwerenga
- D. Tidziwerenga buku loyera usana ndi usiku

KULAMBIRA

Aheberi 4:16 akuti potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa.

OYAMBITSA MPINGO NDIGULU LONSE

Chikhulupiliro chimayenda m'mene munthu umachitira. Zomwe mtima wathu waganiza ndi zomwe milomo yathu imakamba. Oyambitsa mpingo ayenera kumvetsa za malamulo a Mulungu a muchipanngano chatsopano. Zomwe mtumiki achita, ziyenera kufanana ndi zomwe iye mwini amachita. Okhulupilira ambiri saziwa m'mene angayankhire mafunso a mu buku loyera.

1. UTHENGA NDI CHIYANI?

Uthenga ndi mawu amene amapereka chipulumutso ngati tiwagwiritsa ntchito

2. MOYO WOSATHA NDI CHIYANI?

Moyo wosatha ndi chipulumutso cha moyo wa mpakampakamothandizidwa ndi mzimu oyera

Ndikofunika kwambiri kuti oyambitsa mpingo amvetse kwambiri za chipulumutso malingana ndi chipangano chatsopano.

Chipangano chatsopano chinapangidwa ndi anthu opulumutsidwa, komanso ntchito za chipulumutso.

Mtumiki payenkha achite ntchito pokhapokha ngati akhulupilira kuti popanda Yesu anthu sangapulumuke ndipo onse adzalowa mung'anjo ya moto. Inu mumakhulupilira zimenezi.

Oyambitsa mpingo ayenera kumvetsa kuti munthu opanda Yesu ameneyo watayana ndi Mulungu ndipo moyo wake ndiwotaika wamanthawodzadzidwa ndi ziwanda ndipo mzimu wake umakhala wopanda pake.

Ndikofunikira kwambiri kudziwa chifuniro cha Mulungu popeza zochita zathu zimaoneka ngati za uzimu pomwe ndi zachikunja. Yesu Khilisu anatiphunzitsa za kuuka kwake komanso kugonjetsa infa kwake. Iye anati popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi ndipo atafa chiweruzo chidzafika. Aheberi 9:27

Luka 19:10 Yesu anadza kupulumutsa anthu osochera. Uwu ndi udindonso wa oyambitsa mpingo opulumutsa anthu osochera.

Anthu amataika ngati akhulupilira zinthu za m'dziko lapansi osati Yesu.Podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo koma mwachikhulupiliro cha Yesu Khilisu, afedi.

Tinakhulupilira kwa Yesu Khilisu kuti tikayesedwa olungama ndi chikhulupiliro cha Yesu Khilisu ndipo ndi ntchito za lamulo, pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo. Agalatiya 2:16

Ndikofunika kwambiri kuti oyambitsa mpingo ayenera kukhala okhuzidwa ndi anthu otaika kuti nawonso adzapulumuke.

Chisankho chikhale kutumikira komanso kukhala ndi chikhumbo-khumbo chopulumutsa munthu wotaika osati kungotumikira chabe.

Monga oyambitsa mpingo ayenera anthu kuwaika m'magulu komanso kumvetsa zofuna ndi zokonda zawo motsogozedwa ndi mzimu oyera. Choncho ndikofunika kwambiri kuti munthu amvetse kuti akapulumuke

Munthu sangapulumutsidwe ngati salapa machismo ake onse ndi kusawasiya ndikukhulupilira kuti Yesu ndiye Ambuye amene ali mpulumutsi.

Oyambitsa mpingo awonetsetse kuti anthu amene ali ndi chidwi amvetse mbali zonse kutaika ndi kulandira Yesu Khilisu kukhala mpulumutsi wawo.

CHOYAMBA :

Mulapa machimo ndikutani?

Kulapa ndikutembenuka mtima ndikunenetsa kuti ndaleka kenako kumakhulupilira uthenga wabwino nthawi zonse.

Munthu amene walapa machi

Mo ake onse ndikupereka moyo wake onse kwa Yesu Khilisu

KULAPA NDIKUTANI?

CHACHIWIRI:

Kukhulupilira kuti yesu ndi ambuye ndi mpulumutsi.

Ngati munthu adzavomereza mkamwa mwake kuti Yesu ndi Ambuye ndikukhulupilira mu mtima mwake kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa adzapulumuka.

Chikhulupiliro ndi chiyani?

Chikhulupiriro chopulumutsa sichimakhulupirira chinachilichotse chowonjezera pa za chipulumutso. Mwachitsanzo munthu wokhulupirira weniweni samakhulupirira ntchito zake zabwino, samakhulupilira mafano, mayi Maria, Abgelo, Oyera komanso kuti yesu ndi yekha amene ali mpulumutsi, mkhalapakati ndiponso mulungu.

Charles Brock mu buku lake lochedwa kuyambitsa mpingo ananena kuti tantauzo la chipulumutso sinakhudzemo zina ndi zina monga kulapa kukhulupirira komanso machimo zomwe zingachititse kungokhala ndi kagulu kopamphera koma osati mpingo.

Oyambitsa mpingo aliyense ayenera kutsogoleredwa ndi mzimu woyera yekhayo amene amateteza aliyense kuti asachimwe.

oyambitsa mpingo awonetsetse kuti akugawana ndi anzake uthenga mosogozedwa ndi mzimu woyera kuti mau agwire ntcito mmuntima ya .anthu ndikuti ibale zipatso zokhazikika.

OYAMBITSA MPINGO NDI MAUMBONI A ANTHU

Cholinga cha maumboni ndikufuna kugawana ndi anzathu za ukulu wa mulungu. Ndizotheka kumasutsana za zinthu zomwe zinawachitikira ena koma ndikovuta kutsutsana ndi anthu amene sanawachitikira.

Machitidwe 22:1-16, 26:9-23 mtumiki Paulo akunena momveka bwino mmene iye anamulandilira yesu komanso zimene zinamuchitikira atalandira yesu ndikukhala mpulumutsi wake.

1. Zoyenera kukumbukira pamene tikugawana za maumboni

- a) Ukhale wachidule
- b) Kumbikirani kuti cholinga ndi kufuna kupereka chikhulupiriro ku anthu amene sanalandire yesu.
- c) Musalalikire
- d) Musanene zachipulumutso pa nthawi imeneyi
- e) Musaitane anthu ena.

- f) Musagwiritse mau omwe sawamvetsa.
- g) Mukhonza kugwiritsa ntchito ndime zina za buku loyera.
- h) Mukhoza kulemba umboni wanu koma mau asapitilire 250-350
- i) Kenako malizani umboni wanu ndi mau ena amfangitsa chikoka munthu.

2. Umboni

Yankani mafunso otsatirawa okhudzana ndi umboni.

- a) Moyo wanga unali wotani ndisanamulandire yesu. *Machi 22:1-5,26:4-11*

- b) Ndinadziwa bwanji kuti moyo wanga ukufuna ambuye? *Mac 22:6-8, 26-15*

- c) Ndikuti ndipo ndinamulandira bwanji yesu? *Machitidwe 22:6-10, 26:13-18*

- d) Moyo wanga ukusiyana bwanji poyamba ndi tsopano pamene ndinamulandira yesu ndikukhala nkhoswe ya moyo wanga.

3. Mathero

Pomaliza nenani kuti tsopano ndili ndi chikhulupiriro kuti mwalandira mzimu woyera. Mundiore kuti ndilongosolwe za mu buku layera zokhudzana ndi chipulumutso.

Zimene mwachita ndikukhala pakati pa inu munthu wotaika mukatero mwapempha chilorezo chodutsa pa mulatho kukalowa mmoyo mwa munthuyo kapena kukana.

Ngati wavomereza mukhozaa kumulalikira za uthnga wabwino. Ngati wakana mulembe dzina lake kuti mudzimuikiza ma pemphero a tsiku ndi tsiku.

MTUMIKI WOLALIKIRA ZA UMUNTHU

NDIME ZITSANU NDI CHIMODZI ZOMWE ZIKUFOTOKOZA ZA UTHENGA WABWINO

Pali makhalidwe awiri

- i. Chikunja.
- ii. Akhristu.

Pali mfundo za utamiki pofuna kufalitsa uthenga. Chikhalidwe sichingasithe uthenga wabwimo. Chikhalidwe chimangosintha mmene tingapemphelere. Choonadi munthu amachilandira mmene iye aliri komanso mmene akuchilandilira. Ngati kuti umatha kulalikira bwanji koma monga mtumiki umayendera kudziwawa ndondimeko zofuna kulalikira anthu a makhalidwe asiyanasiyana.

KWA ANTHU OSAPEMPHERA

Kwa anthu awa mtumwi ayenera kuyamba ndi mafunso monga ngati, kodi mumadziwa yesu? Nanga mumafuna mutamudziwa mulungu amene analenga dziko lapansi ndi lakumwamba. Kenako mlaliki agwiritse ntchito buku loyera mmene muli nkhani zosiyanasiyana zomulimbikitsa.

KWA ANTHU OPEMPHERA

Funsani funso loti kodi mutamwalira utsuku wa lero kodi mukulowa kuti? Ngati sakutha kuyamika pitirizani ndikupelekera umboni ndipo mugawane nawo uthenga wabwino. Koma ngati ayankha molondola mukhonzanso kumpatsanso mafunso ena angapo monga muli paubale ndi mulungu.

ZOFUNA KUDZIWA

Zokhunzana ndi kumvana mipingo amafitikoza mosiyana. Monga ma Hindul, Budda ndi ena amasiyana ndi Akatolika. Iwo amasiyana potchula za mulungu, yesu, kumwamba komanso kung'anjo ya moto osatha.

Mpingo uliwonse monga mene akumvera. Akatolika amati mulungu ndi mzimi okhaokha ndi wamphamvu zones za dziko lakumwamba ndi lapansi. Yesu ndi mwana wa mulungu amene anamfera, anthu onse pa dziko lapansi.

Kwa a Budda amati kumwamba ndi malo amene anthuangathawireko anthu kukapeza zotsowa zawo.

Nawonso a Hindu amati ndi malo amene tikapeze zotsowa zathu. Koma mpingo wa a ninisiti amati kumwamba ndi malo amene kumapezeka zinthu zonse zomwe kung'anjo sizingapezekeko.

Kulemera sikudzapangitsa munthu kupulumuka. Mipingo yambiribuku la maembo oyerera sibuku lomwe limadziwitsa zinthu. Ambiri mwa iwo sanamvepo za buku loyera.chonco chimene tichite ndikugawana za buku loyera popeza umu ndi mmene mulungu anadziulula kuti iye ndi ndani.

Ena amakhulupirira kuti buku la malembo oyerera ndilo nkhekwe la mawu a mulungu, koma ena ayi. Kwa amene samakhulupilira buku loyerayi mzimu woyera ugwire ntchito mwa iwo ndikuwadziwitsadi choonadi.

Koma anthu musamakangane pokambirana za mawu a mulungu. Chimene mungachite sonyezani chikhulupiliro chanu ndi zimene inuyo mungakhulupilira. Ndikofunika kwambiri kwa mtumiki kuti apeze maumboni amphamvu olimbikitsa anthu kuti nawonso amudziwe.

UTHENGA SUDZASINTHA KOMA MIPINGO NDI IMENE IMASINTHA

CHIKUMBUTSO

Kwa akhiristu tipitilire ndi mawu okudzana za moyo wasatha, koma kwa amene sanadziwe yesu awa pafunaka kuwatenga pang'onopang'ono malingana ndi kumvetsa kwawo.

MENE TINGALALIKIRE UTHENGA WA MULUNGU

1. Cholinga cha Mulungu pa moyo wako

Buku loyera likunenetsa kuti izindakulemberani kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mikhulupilira dzina la mwana wa mulungu. *1 Yohane 5:13.*

Cholinga cha ndime ya baibulo

Pofuna kusonyeza kuti mulungu akufuna kutsimikizira kuti ife ndife opulimutsidwa chifukwa cha chikondi chake.

Kutambasula za ndime ya baibulo

Moyo wosatha uli pawiri.

- a) Kusonyeza kukhala mwa yesu khristu ndi mtendere wake pano pamene tili mmoyo uno. *Yohane 17:3*
- b) Kudzakhala ndi yesu khristu kumwamba pamene tidzafa. *Yohane 14:1-3*

Ndime za baibulo zidzatithandiza bwanji

Kodi mukufuna kukhala ndi chitsikimidzo zikhudzana ndi za mayo wosatha?

Kwa okhulupirira ngakhalenso amene sanamulandire yesu ayenera kufotokozeledwa bwinobwino kuti amvetse.

2. Zofunika

Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemelero wa Mulungu. *Aroma 3:23*

Cholinga cha ndime

Kufuna kusonyeza kuti tonse ndi ochimwa

Tchimo ndi chiyani?

Tchimo ndikupanga zinthu zotsutsana ndi Mulungu. Kodi mwadziwa kuti mwamuchimwira Mulungu?

Nanga mphoto ya chimo ndo chiyani? Buku loyera limanenetsanso kuti pakuti mphoto yake ya uchimi ndi infa koma mphoto yaulele ya mulungu ndi moyo wasatha wa mwa Yesu khristu ambuye wathu.

Izi zimasonyeza kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha Machimo athu.

Imfa ndi chiyani

Imfa imatanthauza kusiyana ndi Mulungu mwa njira ziwiri. Choyamba kisiyana ndi Mulungu pano padziko lapansi. Uwu ndi moyo opanda mtendere mu uzimu ndiponso opanda chikhulupiliro.

Uwu ndi moyo umene ulibe Yesu wa mayankho ndi moyo wasatha mu mtima. Kusiyana ndi mulungu munthu amatsala chabe ndi wamantha.

Chachiwiri kisiyana ndi Mulungu pa moyo wasatha kumwamba ndikulowa ku ng'anjo yamoto wasatha. Uwu ndi moyo womwe ulibe yesu pa moyo wasatha. Imfa inadza chifukwa cha machimo athu ndipo anatilekanitsa ndi mulungu. Ndime imeneyi ikutifunsa kuti, kodi tikuvomereza kuti imfa inadza chifukwa cha machimo athu omwe anatilekanitsa ndi Mulungu?

3. Mphoto ya mulungu

Aroma 5:8, Mulungu akutitsikimizira ife za chikondi chake mwini yekha mmenemo kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Yesu khristu anatifera ife.

Ndime imeneyi ikusonyeza kuti Mulungu amakonda dziko lapansi kotero anapereka mwana wake kudzatifera ife vchifukwa cha machimo athu. Imfa ya Yesu khristu pa mtanda paja ndi nsembe imene inamasula machimo athu. Anthu pano akuyetsera njira zofuna kulumikizana ndi Mulungu.

Ena amayesetsa kufana kulumikizana ndi mulungu popembeza mizimu, zosema, mafano ndi zosiyanasiyana. Munthu payekha alibe mphavu zoti kudziyeretsa tekha popanda mphamvu ya mzimu woyera kuchitapo kanthu. Kudzera mwa ambuye wathu Yesu khristu ndiye yankha yophathana ndi Mulungu

Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machismo athu, anauka kwa akufa ndikugonjesa imfa. Iye ndi wamoyo ndipo akufuna kukhala mwa inu nthawi zones.

Apa tiphunzira kuti Yesu ndiye ambuye, mpulumutsi komanso mphatso yaikulu yochoka ku mwamba.

4. Mayankho

Ngati munthu adzavomereza mkamwa mwake kuti yesu ndiye ambuye ndi kukhulupilira muntima mwake Mulungu anamuukitsa kwa akufa adzapulumuka. *Aroma 10:9.*

Ndime imeneyi ikutiphunzitsa kuti tingachite chiyani kuti timulandire Yesu ndikukhala mbuye wathu. Ikukambanso kuti tilandire Yesu tiyenera kuchita zinthu ziwiri izi:

Choyamba kuti timilandire Yesu tiyenera kulapa machismo athu ndikuyang'ana mtanda wake kenako timusate iye.

Chachiwiri tiyenera kuvomereza muntima mwathu kuti Yesu anauka kwa akufa ndipo ndiye mpulumutsi wathu.

Izi zitithandiza kuti ife tisiye kudalira zina ziri zones za dziko lapansi, ndikudzipereka moyo wathu onse kwa ambuye wathu Yesu khristu.

ZOFUNA KUCHITA

**NJIRA ZOFUNA KUCHULUKITSA
MALO OFALITSIRA
UTHENGA WABWINO**

ZOFUNA KUCHITA

Mugawo ili tiwona oyambitsa mpingo ayenera angatsate. Pali njira zinayi zomwe oyambitsa mpingo angatsate.

Pomanga mpingo ndipo palinso njira zinayi zomwensho oyambitsa mpingo angatsate poyambitsa ndi kuchulukitsa mpingo.

ZOYENERA KUKUMBUKIRA

Pali mfundo zimene zimatisogolera opfuna kusankha njira zochulukitsira magulu opemphera.

Mpingo utha kukula mwa njira zosiyanasiyana. Chifunuka kwambiri ndikutsatira utsogoleri wa mzimu woyera amene amaoeza ali kuphunzitsa atsogoleri amene atsegula mitima yawo kuti akagwire ntchito ya ambuye.

Kumbukirani kuphunzitsa ena

- ✓ Njira zinayi zoyenera kuzitsata pomanga mpingo
- ✓ Njira zomwe oyambitsa moingo angatsate.

NJIRA ZINAYI ZOMWE ZINGATSATIDWE POMANGA MPINGO

GAWO 1: Pofuna kumanga nyumba yopemphereramo tiyenera kuyambira panso kufikira pamene tiyambe kuman ga zipupa.

GAWO 2: Kenako kupitiliza mmene tikufunira maonekedwe a nyumbayo. Pali maonekedwe osiyanasiyana a nyumba ya mulungu koma pano tikambirana mitundu inayi.

1. NYUMBA YA CHITREDITIONOLO

Iyi ndi nyumba imene simarira zambiri. Tchito yake ndi kuphunzitsiramo za malembo oyera.

Imeneyi imayanganiridwa ndi apasitala kapena akulu am-pingo kapenansi a dikoni.

2. NYUMBA YA SETIRAITI

Iyi ndi nyumba ya mulungu imene imagawa chithandizo ku mipingo ya ing'onoing'ono. Opemphera amachoka kumalo osiyanasiyana. Amene amayanganira nyumba imeneyi ndi pasitala amene adalumbiritsidwa.

3. NTUMBA YA SELLO (NTHAMBI)

Iyi ndi nyumba imene anthu amapemphereramo ochokera mmakomo, maofesi ndi malo osiyanasiyana.

Anthju asiyanasiyana monga azimayi, azibambo, anyamata ndi asungwana.


4. NYUMBA

Iyi ndi nyum ba yomwe anthu ochepa monga 15 lapena 30 amakumana kupemphera.


Ntchito ya malo ngati awa ndikubatiza, kupembedzera kufalitsa uthenga, utumiki komanso kukumana a mipingo yosiyanasiyana.

SEKO YA OYAMBITSA MPINGO

SEKO 1 (YOYAMBA)




SEKO 2 (YACHIWIRI)




KUPITIRIZA SEKO 2 (YACHIWIRI)

Chikondwerero cha seko 1 chikhonza kukondwelera lomodzi ndi seko 2 kapena gulu liri lonse pakepake.




SEKO 3 (YACHITATU)




Museko 3 Gulu la uthenga wabwino, chikondwewero, uthenga ndi utumiki ziyenera kuyendetsedwa ndi okhulupirira omwe apezeka mu seko yoyamba ndi yachiwiri mmalo mwa PEL

KUPITILIZA SEKO 3 (YACHITATU)




SEKO 4 (YACHINAYI)




Atsogoleri omwe apezeka komwe gulu la uthenga wabwino anakalarikira tsopano liralikire magulu onse a uthenga wabwino, chikondwewero komanso gulu limeneli liphunsitsidwe mozama kutsogolera mpingo.

KUPITIRIZA SEKO 4




Maseko onsewa akhonza kukhala mpingo umodzi waukulu kapena mipingo inayi malingana momwe magulu anu amakhalira. Atumiki atsopano akhonza kutsogolera maseko onse anayi.


SEKO 5 (YACHISANU)



Mpingo watsopano wabadwa kugwiritsa ntchito njira ya PE.




Kugwiritsa ntchito PE pa nyumba yaikulu yopemphera.



NJIRA YA OIKOS

Anthu amene alandira Yesu Khilisitu chifukwa cha munthu adzetsa mtendere. Koma siokhulupilira kwenikweni.



MASAMBA

Oyambitsa mpingo ndi m'mene angaphunzitsire mawu a Mulungu popanda buku la mawu a Mulungu.

Zipangizo.....

Olemba Thomas Wade Akins

Koma atadza iyeyo mzimu wa choonadi adzatsogolera inu m'choonadi chonse. Pakuti sadzalankhula za iyeyo mwini koma zinthu ziri zonse adzazimva adzazilankhula ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. Yohane 16:13-14. Mzimu woyera ndiye choonadi m'mitima yathu.

Nthawi zina ndinawerenga nkhani ina yake ku Isaya ndipo nkhaniyo inali motere “Ndinayenda patsinje okuya ndipo madzi sananditenge ndipo ndinadutsa pa moto ndipo sunandiotche”. Pophunzitsa ananthu itanani kuti awerenge buku la malembo overa ndipo inuyo mudzifunsa mafunso kuchokera pa nkhani imene yawerengedwa.

Monga mtsogoleri cholinga cha maphunziro ndikufuna kuyankhula ndi Mulungu. Choncho mawu a Mulungu tiyenera kutsatira ndondomeko izi:

GAWO LOYAMBA

Mtsogoleri asankhe ndime iliyonse mu buku loyera.

GAWO LACHIWIRI

Mtsogoleri asankhe m'modzi mwa overa kuti awerenge

GAWO LACHITATU

Mtsogoleri awerengenso malembo omwe awerengedwa kale ndi munthu wina mwamakono

GAWO LACHINAYI

Mtsogoleri afunse mafunso kuchokera pa ndime imene wawerenga kufunafuna choonadi,

Mafunso ake akhale motere:

1. Kodi ndime imeneyi ikutinji za Mulungu?
2. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani za Yesu Khilisitu?
3. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani za machismo?
4. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani pa zakukhulupilika?
5. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani pa za ine?
6. Kodi mu ndime imeneyi ikunena chiyani za chilungamo cha Mulungu?

GAWO LA CHISANU

Mtsogoleri kenako asonyenze omvera ndime zina zofanana ndi imene awerenga kuti omvera afananitse.

GAWO LA CHISANU NDI CHIMODZI

Kenaka mtsogoleri akambirane ndi omvera pogwiritsa dzina lake.

Awafunse omvera kuti ndime yo ikunena chiyani kapena iwo aphunzirapo chiyani pankhani imene yawerengedwa

NDIME YACHISANU NDI CHIWIRI

Mukatha kukambiraza ndimeyo kenako pitilizani kukambirana nkhani zina ndi zina za mawu a buku la malembo oyera .

CHITSANZO

GAWO LOYAMBA

Sankhani ndime yochokera mwina kwa Yohane.

GAWO LACHIWIRI

Sankhani munthu wina kuti awerenge. Yohane 1:1 “Pachiyambi panali mawu ndipo mawuwo ndiye Mulungu”

GAWO LA CHITATU

Kenako mtsogoleri abwereze zimene wina wawerenga monga pachiyambi panali mawu ndipo mawuwo ndiye Mulungu

GAWO LA CHINAYI

Mtsogoleri afunse mafunso

1. Kodi ndime imeneyi ikunena zachiyani za mawu?
2. Kodi ndime imeneyi ikunenanji za Yesu Khristu?

GAWO LA CHISANU

Wina awerenge Yohane 1:14

Mawu amakhala pa ife ndipo chifukwa cha mawu taona ulemelero wa Mulungu. Chifukwa cha mawuwo omwe anachokera kwa Mulungu taona chilungamo chonse. Iye anandiphunzitsa za choonadi.

Kenako funsani mafunso awa:

1. Ndani amene anadzatibadwira pa dziko lapansi
2. Ndani anatifera ife chifukwa cha machismo anthu
3. Ndani anaona ulemelero wa Mulungu
4. Kodi Yohane anaona chiyani?
5. Kodi ulemmerero utanthauza chiyani?
6. China chomwe Yohane anaona ndi chiyani kwa Yesu ?
7. Tchulaninso china chomwe Yohane anaona kwa Yesu?
8. Chifundo ndi chiyani?
9. Nanga chilungamo ndi chiyani?

Kenako tione kuti ndime imeneyi ikuphunzitsa chiyani kwa ife.

Aliyense m'modzim'modzi ayese kuyankha mafunso
Monga mundimeyi tamva :

1. Mulungu ndi chiyambi
2. Mulungu ndo oyamba nndi omaliza
3. Mulungu ndi moyo wosatha
4. Yesu ndi Mulungu
5. Yesu Khilisu ndiye mulengi wa dziko la pansu
6. Yesu ndiye analenga ine
7. Yesu ndiye chikondi chosatha. Iye anandipatsa zomwe sindimayembekezera.

GAWO LA CHISANU NDI CHIMODZI

Kenako chitani chimodzimodzi ndi ndime zina zomwe mungasankhe

GAWO LA CHISANU NDI CHIWIRI

Tsekani ndi pemphero.

Pemphero likhale lopempha mzimu woyera kuti zonse zimene mwawerenga zikhazikike m'mitima mwa omvera.

Pali zipangizo zambiri zomwe tingagwiritse ntchito pophunzitsa mawu a Mulungu koma nthawi zambiri tingagwiritse ntchito buku la malembo oyera.

Nthawi zambiri tigwiritse ntchito mzimu oyera kuti uzititsogolera ndikukhazikika m'mitima yathu.

Mphunzitsi asanene kuti lero sitiphunzira chifukwa choti zipangizo palibe.

Mtsogoleri akhoza kugwiritsa ntchito mafunso. Nthawi zonse lolani mzimu oyera kuti ugwire ntchito mwa inu ndikukusonyezani choonadi.

MATHERO A BUKU LA MAWU A MULUNGU